


# KULIMBIKIRA

 Kawirikawiri timalengeza izo kuti muzikhala otsimikiza kuti mukukumbukira komwe zikakhalire. Ife tikufuna kuti tiwerenge kuchokera ku Mateyu, mutu wa 15 wa Mateyu, kuyambira ndime ya 21.

*Kenako Yesu anachoka kumeneko, ndipo anachoka kupita ku malire a Turo ndi Sidoni.*

*Ndipo, taonani, mkazi wa ku Kanani anatulukira kuchokera ku magombe omwewo, ndipo anafuulira kwa iye, akuti, Mundichitire ine chifundo, O Ambuye, inu mwana wa Davide; mwana wanga wamkazi wagwidwa mowopsya ndi mdierekezi.*

*Koma sanamyankhe iye mawu amodzi. Ndipo akuphunzira ake anadza ndipo anampempha iye, kuti, Mutumizeni iye apite; pakuti akutilirira ife.*

*Koma iye anayankha ndipo anati, Ine sindinatumidwe koma kwa nkhosa zotayika za nyumba ya Israeli.*

*Pomwepo iye anadza namgwadira iye, nanena, Ambuye, ndithandizeni ine.*

*Koma iye anamyankha anati, Sichabwino kutenga mkate wa ana, ndi kuwuponyera iwo kwa agalu.*

*Ndipo iye anati, Zoonadi, Ambuye: komabe agalu amadya...zinyenyiswa zomwe zimagwa kuchokera pagome la ambuye. Kenako anati... .*

*Kenako Yesu anayankha ndipo anati kwa iye, O mkazi, chikhulupiriro chako ndi chachikuru: zikhale kwa iwe ngakhale monga ukufunira. Ndipo mwana wake anachiritsidwa kuyambira ora lomwelo.*

<sup>2</sup> Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero. Ndikudabwa, usikuuno, mitu yathu ndi mitima yoweramitsidwa, ngati pangakhale winawake pano amene akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero. Kodi mungangozidziwitsa pamene mukukwezera manja anu kwa Mulungu, ndikuti, “Ine ndiri ndi chosowa, Ambuye, ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine.” Ambuye akudalitseni inu.

<sup>3</sup> Atate athu Akumwamba, pamene ife tsopano tikuyandikira Ukulu Wanu, mu Dzina la Ambuye Yesu, pakuti Iye anatiuza ife, “Ngati inu mudzawapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, icho chidzaperekedwa.” Ife tikubwera ndi chikhulupiriro chonse chomwe tiri nacho, tikukhulupirira kuti Inu mutiyankha ife molingana ndi zosowa zathu, usikuuno, pakuti ziripo zambiri. Inu mukuona manja a ana Anu kudutsa mchipindachi muno, pamene iwo akukwezera manja awo. Ndipo Inu nokha mukudziwa

chimene chinali pansi pa mtima. Ine ndikupemphera kuti Inu muwayankhe iwo, Atate, usikuuno. Ndipo mulole chokhumba chirichonse chimene iwo ali nacho, chiperekedwe kwa iwo lero.

<sup>4</sup> Ife tikuwapempherera iwo amene ali osapululumutsidwa ndipo sakukudziwani Inu ngati Mpulumutsi wawo. Ife tikupemphera kuti iwo akulandireni Inu, usikuuno, ndi kumpeza wokwanira-mu zonse uyo amene ayenera kukhala naye mu ora la imfa.

<sup>5</sup> Ambiri pano mwinamwake amene anakulandirani kale Inu, ndipo sanadzadzidwebe ndi Mzimu Wanu. Ife tikupemphera, kuti usiku uno, kuti Inu mudzatsanulire mwa iwo unyinjira wa Mzimu Woyera, kuti iwo akakhoze kukhala antchito kwa Inu mu maora awa otsekera a mbiriyakale ya dziko.

<sup>6</sup> Achizeni odwala onse ndi osautsika, Ambuye. Inu mukudziwa chosowa chawo.

<sup>7</sup> Ndipo ife tikupemphera kuti Kukhalapo Kwanu kubwere pakati pathu, usikuuno, mwanjira yakuti ife tikuzindikireni Inu ngati Ambuye wathu wowuka. Ndipo pamene msonkhano udzatsekedwa, ndipo ife nkumapita ku nyumba zathu, mulole tikakhoze kuyankhulana wina ndi mzake, tikunena monga iwo ankachokera ku Emau tsiku lijali, tikuti, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe m’njira?” Pakuti iwo anapangidwa kuti akudziwani Inu mwa chizindikiro chinachake chimene Inu munachichita kusanachitike kupachikidwa Kwanu. Ndipo Inu mutatha kuwuka, Inu munalali Yesu yemweyo, mukuchita zinthu zomwezo. Mulole ife tichitirebe umboni mofanana, usikuuno. Mu Dzina la Yesu, ife tikupemphera. Amen.

Mukhoza kukhala pansi.

<sup>8</sup> Ndatenga nthawi yanga yonse usiku wathawu, pa mutu wakuti *Ife Tikufuna Timuwone Yesu*, ndipo atatha kufotokozeka za chikhalidwe cha misonkhano ndi momwe angavomerezera, monga kawirikawiri M’bale Borders amachitira kwa alendo usiku uliwonse kuyambira pano. Ndinapita nthawi yanga yonse, mpaka hafu pasiti-naini, ndipo sindimakonda kuwadikiriritsa anthu. Mawu pang’ono chabe, kuti tidziwane, ndipo kenako Mawu a Ambuye amatanthauza. . . Nthawi ina, Iye kuyankhula, zimatanthauza kuposa momwe aliyense anganenera mu nthawi ya moyo, Mawu amodzi okha ochokera kwa Iye.

<sup>9</sup> Ine ndikukhumba kuti nditenge monga momwe izo zinakhalira, usikuuno, mutu wochokera mu kuwerenga kwa Lemba uku kumene Mulungu watipatsa ife pano ngati nkhani yake. Mulole Iye apereke ilo kwa ife. Ndikufuna nditenge mawu amodzi: *Kulimbikira*.

<sup>10</sup> Mawu, malingana ndi Webster, pa zolemba zina zomwe ine ndazilemba kwa apa, izo zikutanthauza “kukhala ndi khama,”

kukhala *wolimbikira*, ndipo, ndiko kuti, ukufika pa cholinga; “kukhala wakhama,” ndipo ndiko *kulimbikira*.

<sup>11</sup> Munthu wa mibadwo yonse, amene amakhala ndi chikhulupiriro mu zimene iwo akuyesera kuti apindule, wakhala ali wolimbikira. Palibe munthu amene angakhale wolimbikira pokhapokha atadziwa kaye zomwe akuyesera kuti akwaniritse. Ndipo poyamba iwe umayenera kudziwa zomwe ukuyesera kuti uzikwaniritsezo, ndipo kenako umakhala ndi chikhulupiriro kuti upeza zomwe ukuyeserazo. Ndipo zimenezo zimakupangitsa iwe kulimbikira, chinachake chimene ukudziwa kuti ndi chenicheni.

<sup>12</sup> Chikhulupiriro chimakhazikitsidwa mwanjira imeneyo. Chikhulupiriro sichimakhazikika pa nthano chabe ndipo pa chinachake chimene, chabwino, chimene chimangoti, “pita ukachite izi kapena ukachite *izo*,” pa mawu a munthu wina. Koma chikhulupiriro chimatenga malo ake a mpumulo Amuyaya pa Mawu a Ambuye, pa Mawu a Mulungu, amene ali Baibulo.

<sup>13</sup> Tsopano ife timakhulupirira Baibulo kukhala Mawu osalephera a Mulungu. Ife timakhulupirira kuti Ilo ndi vumbulutso lonse la Yesu Khristu; akudziulula Yekha mu Chipangano Chakale, kudzera mwa aneneri; Mulungu akudzizindikiritsa Yekha kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu, ndipo mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu, mthupi. Iye anapachikidwa chifukwa cha machimo athu; anafa, anaikidwa mmanda, anauka tsiku lachitatu, anakwera Kumwamba, ndipo wabwerera kuno kachiwiri mu Dzina la...Mmawonekedwe a Mzimu Woyera, Mulungu akukhala...Nthawi ina, Mulungu pamwamba pathu; mwa Khristu, Mulungu nafe; tsopano Mulungu mwa ife. Ndi Mulungu akugwira ntchito njira Yake yobwererera mwa munthu, kuti azidzapembedza, kuti azidzapembedzedwa kupyolera mwa munthu, nthumwi ya Mulungu. Mulungu samachita kalikonse kunja kwa munthu kukhala wothandizira Wake, mthandizi Wake.

<sup>14</sup> Ndipo tsopano munthu amene wakhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, wakhala ali wakhama kwambiri pa zimene iwo akuyesetsa kuti achite. Ndipo timamutenga munthu wa kayendedwe konse ka moyo.

<sup>15</sup> Mwachitsanzo, George Washington, kuno ku Valley Forge. Atha kupemphera usiku wonse mu chipale, mpaka m’chiuno mwake, anali atanyowa kwambiri m’chiuno mwake, ndipo mtsinjewo unali wodzaza ndi ayesi. Koma iye anagwira masomphenya ochokera kwa Mulungu, iye anagwira chikhulupiriro, kuti Mulungu akanati adzamupatse iye chigonjetso. Ndipo a—mtsinge unali... sindikanakhoza kukhala ndi ayesi wochuluka mmenemo, chonchobe. Oposa magawo awiri mwa atatu a ankhondo ake analibe ngakhale nsapato kumapazi awo. Mapazi awo anali atakulungidwa mu nsanza,

atayima mu chisanu chimenecho. Komabe iye anamverera mu mtima mwake kuti Mulungu anali atamupatsa iye chigonjetso. Iye anali atapemphera mobowoleza. Tsiku lotsatira, ife tikudziwa, zipolopolo zitatu za mfuti zinadutsa mmalaya ake osamukhudza iye. Ndipo mtsinje sukanakhoza kumuletsa iye, ngakhalenso chipolopolo cha mfuti sichikanakhoza kumuletsa iye. Iye anali wakhama, chifukwa iye anali atapemphera mobowoleza. Ndipo anali nacho chikhulupiro mu chimene iye anali kuchita, mwa Mmodzi yemwe anali kumutsogolera iye, ameneyo anali Mulungu.

<sup>16</sup> Palibe chimene chingamulepheretse munthu pamene iye— iye amakhala wolimbikira, pamene wadziwa chimene akuchita, ndipo amakhala ndi chikhulupiro mu zimene iye akuyesetsa kuti akwaniritse.

<sup>17</sup> Imodzi ya nkhani zakale kwambiri mu Baibulo, imodzi ya izo, inali ya Nowa. Nowa sanangokhala munthu wina wosiyana. Iye anali munthu wamba, mwinamwake mlimi.

<sup>18</sup> Ndipo dziko linali lauthakati, monga momwe liri lero, lodzaza ndi sayansi ndi anthu otchuka. Iwo anali atatumphuka kuchokera kwa ana a Kaini. Ana a Seti anali azibusa odzichepetsa, alimi. Koma ana a— a Kaini anali anthu anzeru, omanga, ndi—ndi oyambitsa, ndi asayansi, anzeru kwenikweni, achipembedzo chenicheni. Ndipo iwo anali nawo mawonekedwe awo aumulungu, koma anali kukana, monga momwe zikumakhalira lero, mphamvu ya Mulungu.

<sup>19</sup> Ndipo Nowa pokhala munthu wolungama pamaso pa Mulungu, tsiku lina Mulungu anakomana naye iye kuthengo ndipo anayankhula naye iye, ndipo anamuuzza iye kuti amange chombo, chifukwa Iye anali woti awononga dziko ndi madzi.

<sup>20</sup> Tsopano izo zinali mwamtheradi zotsutsana ndi miyeso yonse ya sayansi ya tsiku limenelo. Mwaona, iyo inali isanavumbepo. Pamenepo—munalibe chinyontho mu mlengalenga. Ndipo Mulungu anali atalithirira dziko lapansi kudzera mu ulimi wothirira, chokwera kudutsa pa dziko lapansi, ndi akasupe. Ndipo kunalibeko madzi ochitira zimenezo, munalibe madzi mu mlengalenga.

<sup>21</sup> Sayansi mu tsiku limenelo mwina inali yokhoza kwambiri. Iwo anapindula kwambiri nthawi imeneyo kuposa iwo— akukhoza kuzifotokoza lero. Iwo ankamanga mapiramidi mu Igupto, ma sphinxes. Iwo sangakhoze konse kumanga zimenezo leronso. Miyala imeneyo kukwera chomwecho mu mlengalenga, ife tiribe chinthu choyikira izo mmwamba umo, kapena tiribe mphamvu yoti anyamulire izo. Koma mwanjira ina iwo amatha kukwaniritsa zimenezo mmasiku a Enoki ndi Nowa, chigumula chisanachitike. Ndipo mwinamwake iwo ankawombera mwezi, ndipo mwina anali nawo akasidi, ndi zina zotero. Ife sitikudziwa.

22 Koma Yesu anati, “Monga mmene izo zinali mmasiku a Nowa,” chitukuko chachikulu chanzeru monga chinali nthawi imeneyo, “chomwechonso zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu.”

23 Ndipo tsopano mwina iwo, mu kafukufuku wawo wa sayansi, iwo—iwo anapeza chinachake kumeneko chimene akanatha kupanga utoto umene ungakhalepo mpaka lero, utoto wamtundu wina, umene sumatuwa.

24 Ndipo iwo amakhoza kuwumitsa thupi, kuumitsa mtembo, womwe ungamawoneke mwachibadwa ndithu; komabe lero, pambuyo pa zaka zikwi zinayi, iwo akuwonekabe mwachibadwa. Ife sitingakhoze kuchita zimenezzo ngati titafuna kutero. Ife tiribe kanthu kochitira izo. Tinataya lusolo, luso lochuluka lalikulu limene iwo anali nalo.

25 Mosakayika iwo anali ndi zida zotsimikizira kuti mumlengalenga munalibe madzi. Ndipo munthu uyu akubwera pamenepo, motsutsana ndi sayansi, ndipo akudzanena kuti, “Kudzatuluka madzi kuchokera mmiyamba.”

26 Tsopano, sayansi ikhoza kutenga chida ndi kuchiwombera mmwamba mu mlengalenga, ndi kuti, “Tayang’anani apa, Nowa, tawerenga chida ichi. Izo zimapereka pa choyezera ichi apa, kaya muli madzi aliwonse mmwamba umo, kapena ayi, ndipo kulibeko aliwonse. Tsopano iwe ukuti alipo mmwambamo, ndipo komabe kafukufuku wa sayansi akusonyeza kuti iwo kulibeko.”

27 Izo sizinamuletse Nowa. Anali wakhama. Iye ankadziwa kuti Mulungu anati, “Idzavumba mvula,” ndipo Mulungu anali wokhoza kuiyika mvula mmwambamo ngati Iye ananena chomwecho. Iye akanaipanga iyo, kaya inalipo iliyonse kumeneko kapena ayi. Chotero iye anali wakhama atawadziwa Mawu a Ambuye.

28 Ndipo pamene munthu awadziwa Mawu ndi chifuniro cha Mulungu, iwe umadzakhala wakhama. Iwe umadzakhala wolimbikira. Ziribe kanthu zomwe sayansi ikunena, “Chabwino, iwo sangakhoze kuchita *izi*, iwo sangakhoze kuchita *zimenezzo*,” iwe ukudziwa izo, mulimonse. Iwe wagwira Chinachake, ndipo Chinachake chimenecho chakugwira iwe. Iwe ukuzungulira nacho limodzi. Iwe, pali chinachake cha icho, chimene iwe sungakhoze kuchifotokoza icho. Ziribe kanthu momwe zikuwonekera mwasayansi kukhala zabodza, komabe pali Chinachake mmenemo chimene chimakuuza iwe kuti ndi Mulungu, ndipo palibe chimene chiti chidzayimitse icho.

29 Chotero ife tikupeza kuti Nowa ankapitirira kumakhoma chombo, panalibe kanthu kuti umboni wasayansi unali wochulukuka bwanji, “sizinali chomwecho, ndipo kunalibeko mvula.” Ndipo anakhulupirira izo mulimonse, chifukwa iye anali atamva Mawu a Ambuye.

<sup>30</sup> Ndipo apo ndi pamene chikhulupiroro chimakhazikika mwaulemu, PAKUTI ATERO AMBUYE.

<sup>31</sup> Mose, munthu wina wamkulu, wanzeru yemwe analeredwa, wobadwira mdziko chifukwa cha kupindula kwina kwake kwa Mulungu. Ndipo anayetsa kukwaniritsa cholinga ichi ndi zochita zake zasayansi. Iye timaphunzitsidwa ndi kuuzidwa ndi mbiriyakale kuti anali mtsogoleri wopambana wankhondo, ndipo njira yake yokhayo yochitira chirichonse, inali, kupha. Iye anali wanzeru kwambiri mwakuti amakhoza kuwaphunzitsa Aigupto anzeru, nzeru. Mu nzeru zake zonsezo ndi zonse zimene iye ankazidziwa, komabe iye analephera, analephera momvetsa chisoni, kuti akwaniritse zimene Mulungu ankafuna kuti iye achite. Ndipo pakupeza kulephera kwake, pakumupha M'igupto ndi kumubisa iye mu mchenga, ndi kumvetsera chidzudzulo kuchokera kwa mbale wake, kapena funso, “Kodi utipha ife monga unamuphera M'igupto uja?” Chifukwa cha ichi, Mose anathamangira m'chipululu, mneneri wothawa.

<sup>32</sup> Zitatha zaka forte ali mu chipululu, zimene Mulungu anali akumuchotsa maphunziro kumuchotsa zinthu za mdziko, kupita naye ku malingaliro a Mulungu; kumulanda digiri yake yonse ya udokotala, ndi chirichonse, kutali ndi iye, kufikira kuti Iye adzakhoze kugwira ntchito mu mtima mwake.

<sup>33</sup> Pamene Iye anali atakonzeka ndi zida, tsiku lina pamene iye anali kuweta nkhoa kuseri kwa chipululu, njira yakale yodziwika, iye anawupeza mtengo ukuyaka moto.

<sup>34</sup> Mose, pokhala wasayansi, iye sanawufikire konse iwo mwanjira ya sayansi. Ngati inu mungazindikire, ngati iye akanakhala kuti anali wasayansi, iye akanati, “Tsopano nditenga ena a masamba a mtengowo, ndipo ndiwatengera iwo ku labotare ndi kukapeza chimene iwo anapoperapo, chifukwa chimene iwo amayaka ndipo osapsya.” Ngati akanachita zimenezo, ndiye kuti anali asanakonzekabe.

<sup>35</sup> Koma chimene iye anachita, iye anachiyandikira Icho ndipo anavula nsapato zake, anagwada pa mawondo ake ndipo anayamba kuyankhula kwa Icho, chifukwa iye ankadziwa kuti Icho chinali chazimu. Kuchokera kumeneko kunadza Mawu a Ambuye, akuti, “Ndamva kubaula kwa anthu Anga, ndipo ndakumbukira Mawu Anga. Ine ndikukutuma iwe kuti ukawawombole iwo.”

<sup>36</sup> Tsopano nthawizina, mu njira ya ntchito, Mulungu amamuitana munthu Wake kuti akachite zinthu izo ndi zopusa mwamtheradi ku malingaliro achithupi. Iye amawapangitsa iwo kuchita chinthu chomwe chimasanduka chosketsa. Mwachitsanzo, bwanji ngati Mose akanalephera, monga mnyamata wa zaka forte, msilikali; ndi mpandowachifumu, phazi lake pamenepo, ndi ankhondo onse a Igupto ali pansa pa ulamuliro wake? Ndipo kuti alephere kuchita zimenezo, ndipo

apa iye akupita ku Igupto, mmawa wotsatira, atatha kukumana ndi Mngelo uyu mchisamba, wopanda kanthu m'dzanja lake koma ndodo yakale yokhota ya m'chipululu, ali ndi mkazi wake atakhala pa bulu, ndi Gershom pa ntchafu yake, ndevu zoyera zikulendewera pansu mchiuno mwake, mwinamwake. Anali ndi zaka eyite zakubadwa. Mutu wake wadazi ukuwala ku dzuwa, ndi ndodo m'dzanja lake, maso ake akuyang'ana mu mlengalenga, ndipo akumwetulira pamilomo yake.

Winawake ayenera kuti anati, “Mose, ukupita kuti?”

Anati, “Ine ndikutsikira ku Igupto, kukalanda.”

<sup>37</sup> Pamene iye sanakhoze kuchita zimenezo ali ndi ankhondo, akachita bwanji zimenezo ndi ndodo yokhota? “Oh, bambo, mwasokonezeka mmaganizo. Ndinu—mwazungulira mutu.”

<sup>38</sup> Kunali kuwukira kwa munthu mmodzi. Koma chinthu chake chinali, iye anachita izo, chifukwa chakuti anali Mawu a Ambuye. Ndipo Mose anali wotsimikiza, zinalibe kanthu zomwe zotsutsa zinali. Mulungu anali ndi iye, ndipo Iye ndi woyenera kwambiri kuposa zotsutsa zonse.

<sup>39</sup> Ngati amuna ndi akazi akanangoganiza zimenezo usikuuno, kuti Mawu a Ambuye ali Choonadi! Palibenso china. Umuyaya wonse umadalira pa Mawu. “Palibe Mawu amodzi,” Yesu anati, “adzalephera. Miyamba ndi dziko lapansi zidzatero, koma Iwo sadzatero.”

<sup>40</sup> Mose anapita kumeneko. Ndipo anali wakhama kwambiri pamene anaponyera pansu ndodo yake, ndipo inasanduka njoka.

<sup>41</sup> Kenako iye anapeza otsanzira. Izo zikadali panjirabe ya Mulungu, winawake kuyetsa kuti atsanzire chinachake. Ndipo otsanzira anabwera kudzapanga chiwonetsero pa icho, anadzaponyera pansu ndodo zawo.

<sup>42</sup> Mose ankadziwa Yemwe iye anayankhula naye. Iye ankadziwa Yemwe iye anamukhulupirira, ndipo anali wokakamizika kuti Iye anali wokhoza kusunga chimene anachipereka kwa Iye motsutsana ndi oralo. Mose anima njii. Kenako njoka ya Mose inadzameza njoka za amatsengawo.

<sup>43</sup> Ndipo ife timaphunzitsidwa kuti chinthu chomwe chomwecho chidzabwereza kachiwiri, mwinamwake osati mwanjira yomweyo, koma izo zidzabwerezanso kachiwiri mmasiku otsiriza. “Pakuti monga Yane ndi Yambre anamutsutsa Mose, koteri iwo adzakaniza Choonadi.”

<sup>44</sup> Mose anali wakhama, pakuti iye anali nako kupindula, ndi PAKUTI ATERO AMBUYE kumbuyo kwake, “Ine ndidzakhala nawe.”

<sup>45</sup> Davide, atayima pamaso pa Sauli, tsiku lina. Ndipo iye anamva Goliati akutulukira pamwamba pa phiri, chimphona chachikulu chimene chinali ndi zala za mainchesi fortini. Ndi nkondo waukulu m'dzanja lake, usinkhu wa singano

yolukira nsalu, mwinamwake mapazi twente kapena sarte, nkondo waukulu kumapeto kwake, kapena, nsonga, mkuwa. Tangoganizani zomwe mutu wa munthuyo ukanakhala, icho chikanakhala—kukula kwa bafa, ndi chisoti chachikulu chokandapala mainchesi awiri pamwamba pake, ndi mkuwa, zonse zitaphimbidwa. Ndipo anali kutsutsa magulu ankhondo a Mulungu! Ndipo anazinena izo pamaso pa Davide.

<sup>46</sup> Ndipo Davide anali munthu wamng’ono, wofiira, kamunthu kakang’ono, mwinamwake wamapewa-akugwa. Baibulo linati iye anali “wofiira,” kamunthu kakang’ono. Analibe maphunziro ayi—mu kumenyana, ndi mikondo ndi zinthu. Koma iye anali akuweta nkhusa kuseri kwa chipululu, ndipo mkango unabwera ndipo unadzatenga mmodzi wa ana a nkhusa ake, ndipo anamtsatira iye ndipo anakamupha iye ndi legeni. Ife tikuchipeza chimbalangondo chinatero, chinayesera chinthu chomwecho, ndipo Davide anachigonjetsa icho.

<sup>47</sup> Ndipo kenako Davide anati, “Kodi inu mungoimirira ndi kulola Mfilisti wosadulidwa ameneyo azinyoza ankhondo a Mulungu wamoyo?” Iye anawachititsa manyazi abale ake; pamene iwo ankati iye ndi wopusa, iye anali atatulukira kuti adzawonerere nkondoyo. Chikhalirenicho panali Chinachake mwa Davide, chimene iye ankachidziwa kuti iye anali woposa mgonjetsi. Chotero iye anati, “Ngati inu mukuwopa kulimbana naye iye, ine ndipita ndikamenyane naye iye.”

<sup>48</sup> Sauli, akubwera kwa wamkulu wankhondo, Sauli, ndipo anadzaika zida zake pa iye, ndipo izo sizimamukwana iye. Iye anapeza kuti chovala chake chachipembedzo sichinamukwane munthu wa Mulungu. Ndipo chinthucho sichinatero. Iye sanadziwe choti achite. “Izi, sindinatsimikizirepo izi. Ine sindikudziwa kanthu za izi, Bachelor of Art, ndi zina zotero. Chichotsenipo chinthucho pa ine ndipo mudirole ine ndipite mwanjira imene Mulungu anandipatsira ine chiwombolo. Mudirole ndipite ndi legeni.”

<sup>49</sup> “Bwanji,” iwo anati, “iye ndi wankhondo kuyambira ubwana wake, ndipo sindiwe kanthu koma mnyamata.”

<sup>50</sup> Iye anati, “Ndine woposa wofanana naye. Ndiroleni ine ndipite.” Ndipo zinalibe kanthu momwe chimphonacho chinkawonekera chachikulu, komanso momwe chinkawonekera kuti sichinali chenicheni, Davide anachita khama kuti Mfilisti wosadulidwa uja sanyoza ankhondo a Mulungu wamoyo amene iye ankawaimirira.

<sup>51</sup> Oh, ngati ife tikadakhala ndi a Davide ochuluka mwa ankhondo awa, ngati tikadakhala ndi amuna ochulukirapo omwe akanayima ndi kukhala akhama, kulimbikira mu Chikhulupiriro chimene chinaperekedwa kamodzi kwa oyera!

<sup>52</sup> Samsoni, munthu wina wolimbikira kwambiri. Iye anabadwa kubadwa kwa Mnaziri.

53 *Mnaziri* amatanthauza “kupatiwidwira ku Mawu.” Ndi chinthu chabwino bwanji chimene chikanakhala usikuuno ngati Akhristu onse akanakhala Anaziri kwa Ambuye; olekanitsidwira osati ku tizikhulupiriro, koma kwa Mawu. Khristu ndiye Mawu amenewo. Olekanitsidwira ku Mawu!

54 Iye anali ndi mangongo seveni a tsitsi lomwe linkalendewera kunsana kwake, chimene chinali chizindikiro chakuti anali wolekanitsidwa.

55 Ndiyeno tsiku lina iye anakumana panja—mzigwa, wopanda kalikonse m’dzanja lake koti amenyere nako, ndi Afilisti chikwi. Afilisti amenewo anali anthu ngati khoma la mkuwa; zisoti zazikulu zolemera pamitu pawo, zida zazikuru patsogolo pawo, ndi zishango, zomangira, ndi zina zotero, pa, kuti azizembera chipolopolo chirichonse; mwinamwake chisoti chokhala nchichi wake ichesi, pa mitu yawo.

56 Samsoni analibe kalikonse, koma ankawonabe kuti lonjezo limene Mulungu anamulonjeza iye linali lidakali pamutu pake. Iye amakhazabe kumverera kudzoza, mwa kuyankhula kwina. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali ndi iye, pakuti iye ankawamverera mangongo amenewo akulendewera pansu pa mapewa ake. Iye anagwira chimene chinali mwake... akanakhoza kuchipeza, ndipo icho chinali fupa la chibwano cha bulu. Ndipo iye anayima ndi chimenecho mdzanja lake, ndipo anachita khama kuti chisakhale fupa la nsagwada kapena nkono wake womwe, koma idzakhale mphamvu ya Ambuye. Ndipo mphamvu ya Ambuye inabwera pa iye, ndipo iye anakantha, ndi fupa la nsagwada limenelo, Afilisti chikwi.

57 Kodi anachita motani zimenezo? Fupa limenelo, lolimba, lonyowa—m’chipululu, lachibwano, mukhoza kulimenyetsa ilo pa thanthwe, ilo likhoza kuwuluka mzidutswa; ndipo pa zisoti zimene zinali pa Afilisti aja, zimene zinkalendewera pansu, ndi masamba akuluakulu atamamatira mmbali pamene izo zinkapita kudutsa pamapewa, kukhuthala kwa inchi, ndi mkuwa. Iye anayima ndi fupa la chibwano ichi ndipo anagwetsera pansu chikwi. Iwo amati, “Mzimw wa Ambuye unadza pa iye.” Iye anali wakhama.

58 Tsiku lina, mkango unamuthamangira iye ndipo analibe kalikonse mdzanja lake. Koma Mzimw wa Ambuye unadza pa iye, ndi mangongo ake atapachikidwa pa phewa lake, anawung’amba mkangowo ndi manja ake. Iye anali wakhama kwambiri, chifukwa iye ankadziwa kuti lonjezo la Mulungu linali ndi iye. Iye anali wokhoza kukwaniritsa chirichonse, pakuti lonjezo la Mulungu linali ndi iye, kuti awombole.

59 Yohane anali wotsimikiza kwambiri! Yohane M’batizi, pamene iye anabadwa, iye ankadziwa kuti iye anali woti adzakhale ameneyo, atakula mokwanira kuti akumvetsetsa, pafupifupi usinkhu wa zaka naini. Abambo ake anali wansembe.

Kawirikawiri iwo amatsatira mzere wa bambo. Koma sanapite ku masukulu ndi maseminare, chifukwa ankadziwa kuti ntchito yake inali yofunikira kwambiri. Iye anali woti adzamulengeze Mesiya. Iye tikudziwa kuti Mngelo anali atanena chomwecho.

<sup>60</sup> Iye ankadziwa kuti iye anaimiridwa mu Lemba, “Liwu la wina wofuula mchipululu, ‘Kudzakonza njira ya Ambuye!’” Iye ankadziwanso kuti Malaki, zaka foro handiredi zisanachitike, anali atanena kuti, “Taonani, ndidzatuma wamthenga Wanga patsogolo pa nkhope Yanga.” Atatha kukhala mchipululu, kumene, iye analandira maphunziro ake kuchokera kwa Mulungu, osati kuchokera ku seminare ina ya zaumulungu monga kunachokera abambo ake.

<sup>61</sup> Koma anali ndi ntchito yofunikira kwambiri. Iye anali woti adzamulengeze Mesiya, ndipo ankayenera kuti adzadziwe mtundu wa chizindikiro chimene chiti chizidzamutsatira Mesiya. Ndiye iye anazindikira, tsiku lina, iye anali atayima, akulalikira kwa anthu, iye anati, “Pali Mmodzi waima pakati panu tsopano, Yemwe inu simukumudziwa, Yemwe nsapato zake sindiri woyenera kuzimasula, Iye adzakubatzani inu ndi Mzimu Woyera ndi Moto.” Anali wotsimikiza za udindo wake, anali wotsimikiza za utumiki wake, mpaka iye anati, “Iye wayima pano penapake tsopano, pakati panu!” Iye samachita mantha kunena izo pamaso pa Afarisi ndi Asaduki, ndi—ndi asilikari, ndi china chirichonse chimene chinali. Ena a iwo anali atamuyembekezera Iye kwa zaka zikwi, koma iye anati, “Iye wayima pakati panu.” Palibe amene akanatha kumulanda izo. Anali wakhama. Iye anali wolimbikira pamaso pa onsewo. Inde.

<sup>62</sup> Mkazi wamng’ono wa Chigriki uyu, mosakayika, anali atamva za Iye, anamva za Yesu, chitsitsimutso chachikulucho. Mneneri wachinyamata akufika ku Galileya, wochokera ku Nazarete, ndipo anali akusonyeza zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Iye anamva za Iye, ndipo, “chikhulupiriro chimadza pakumva.” Mkazi uyu wa Chisirofonika, pokhala Mgriki. Chikhulupiriro chimapeza magwero omwe ena samawona. Pamene iye anamva, iye anakhulupirira. Iye mwinamwake anamva kuti mtsikana wa oyandikana nawo anachiritsidwa ku khunyu, chimene mwanayo anali nayo, ndipo ayenera kuti anamva za khunyu ili kuti lachiritsidwa. Chotero mwana wake wamkazi anafunikira kuchiritsidwa, ndipo anamva kuti Yesu akanatha kuchita zimenezo.

<sup>63</sup> Pakuti, Iye anali Mawu a Mulungu atasandulika thupi! Yohane Woyera 1, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndiwo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhazikika pakati pathu. Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!” Iye anali pamenepo kuti adzawulule malonjezo a Mulungu a tsiku Lake.

<sup>64</sup> Iye ali pano usikuuno kuti adzatsimikizire ndi kudzawulula

lonjezo lirlonse limene Mulungu anapanga kwa m’badwo uno. Iye ali pano kuti adzachite zimenezo. Iye analipo mmasiku a aneneri. Iye analipo mwa Mose, Iye analipo mwa Davide, Iye analipo mwa Eliya, Iye analipo mwa ena onsewo, kuti adzawulule lonjezo la Mulungu la m’badwo umenewo. Mulungu anawaika Mawu Ake kwa m’badwo uliwonse, ndipo Iye amatumiza mneneri, ndipo Mawu amapita kwa mneneri ndipo amadzawongola izo, ndipo ndicho chimodzimodzi chimene Iye wachita kudutsa mmibadwo yonse. Ndipo Iye ndi Mulungu, ndipo samasintha ayi. Yesu Khristu ndi Mneneri uja usikuuno yemwe wayima pakati pathu. Iye ndi Iyeyo pano mmawonekedwe a Mzimu Woyera, Amene amadziwa chirichonse, ndipo akhoza kuwulula chirichonse chimene Iye akukhumba kuti achichite.

65 Anakhulupirira izi, mosalabadira kanthu kuti anthu sanakhulupirire izo.

66 Chikhulupiriro chimapeza gwero lomwe anthu ena sadziwa kalikonse kake. Pamene munthu akhala ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, iye amagwira chinachake chimene iye sangakhoze kuchifotokoza icho. Ndi chinachake chimene iye wachigwira. Iye sangakhoze kuchikankha, kapena kuchifoshola icho, kapena kuchikoka icho. Izo zimatengera Iye. Ndiyo njira yake ya chikhulupiriro, pamene munthu akhaladi kwenikweni ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, amapeza gwero limenelo limene ena samaliwona.

67 Mawu Ake ndi lupanga. Baibulo linanena chomwecho. Mukufuna kufotokozerwa kwa izo, ndi—ndi Ahebri 4:12, pakuti ndinalemba mutuwo. Baibulo linati, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse.” Lupanga ili liyenera kugwiridwa ndi dzanja la chikhulupiriro. Dzanja la zafioloje silingachite izo. Izo ziyenera kutengera dzanja la chikhulupiriro, kuphunzitsidwira mu zinthu zauzimu, zimene zimamudziwa Mulungu.

68 Apanso, mwina, monga ine ndinganene izi. Kodi mumakhulupirira bwanji kuti Yesu ankayang’ana pa omvetsera ndi kumazindikira maganizo awo? Chifukwa Iye anali Mawu. Tiyeni tibwereze Mawu ena onse apa, “Akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, Wozindikira maganizo ndi zolinga za mu mtima.” Iye anali Mawu. Ndi chifukwa chake Iye ankakhoza kuzindikira malingaliro amene anali mu mtima mwawo.

69 Usiku wathawu, monga ife tinatenga, “monga izo zinali mmasiku a Sodomu,” ndinawonetsa Munthu uja atayima pamenepo, akudya nyama ya ng’ombe, akumwa mkaka wa ng’ombe, akudya mafuta ndi mkate; atayima pamenepo akudya, atavala zovala monga inu ndi ine, atatembenezira nsana Wake ku hema, ndipo anazindikira chimene Sarah anali kulingalira

mu hemamo. Nzosadabwitsa Abrahamu anamutcha Iye Elohim, “Wokwanira Mu Zonseyo, Amene-amakhalapo Yekha,” *Elohim*.

<sup>70</sup> Yesu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala pa kubweranso kwa Mwana wa munthu.” Izo zidzakhala chinthu chomwecho. “Mmasiku,” kodi munazindikira, “ku Sodomu uko”? Izo zimanenedwa mu Luka 17:15, izo zimanenedwa kuti, “Pamene masiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala ziri pakudza kwa Mwana wa munthu, pamene Mwana wa munthu adzawululidwa.” Mmasiku amene Mwana wa munthu akuwululidwa monga Iye anali ku Sodomu, chinthu chomwecho chidzakhala chikuchitika.

<sup>71</sup> Ife tikupeza kuti moto wakonzeka, mafuko akonzeka, alaliki apita ku malo awo, ndipo mphatso iliyonse yakhala mu dongosolo. Nzosadabwitsa ife tiyenera kukhala akhama! Nzosadabwitsa ife tiyenera kukhala olimbikira! Tili ndi cholinga choti tichikwaniritse kwa Mulungu, ndicho, kumuitana atuluke Mkwatibwi wa Yesu Khristu kuchokera ku zipembedzo zonse, kuchokera kwa anthu onse, anthu olekanitsidwa a Mulungu.

<sup>72</sup> Mgriki uyu anali atamva mawu awa. Iye ankawakhulupirira iwo. Iye anali ndi zopinga zambiri, koma chikhulupiriro chake chinalibe chirichonse. Chikhulupiriro sichimadziwa cholepheretsa. Chikhulupiriro chake chinalibe cholepheretsa. Iye anali nacho, koma chikhulupiriro chake chinalibe. Inu mukhoza kukhala nazo zolepheretsa, koma, ngati muli ndi chikhulupiriro, icho sichimadziwa kugonjetsedwa. Chimakhala chotsimikiza. Tiyeni tiwone zina mwa zolepheretsa zake, kwa mphindi chabe.

<sup>73</sup> Ena a iwo mwina anati, “Uzikumbukira, kuti ndiwe wa mtundu wina. Iwe ndiwe Mgriki, fuko la Surofonika. Iye ndi Myuda.” Mwakuyankhula kwina, lero munganene kuti, “Chipembedzo chanu chiribe chitsitsimutso ichi.” Izo sizikupanga kusiyana kulikonse, chipembedzo chanu, kaya icho chiripo kapena ayi. Mkazi ameneyo sanasamale kuti chinali chipembedzo chandani. Iye anali munthu wokhalapo wolengedwa ndi Mulungu, ndipo iye anali nacho chosowa, ndipo iye anali nacho chikhulupiriro ndipo iye akanakachipeza icho. Kaya chipembedzo chake chinali kugwirizana kapena ayi, sizinamupangitse iye kusintha. Iye anawuyambapo.

<sup>74</sup> Ayenera kuti anali ndi wotsutsa wina yemwe mwina anakumana naye pa mzerewo, ndipo anati, “Bwanji, masiku a zozizwitsa anapita. Ife sitikumakhalanso ndi zozizwitsa pano.” Ameneyo akanakhoza kukhala Myuda, iye atalowa mkati, iye uko mdziko ili kumene Yesu anali, kutsidya kwa Galileya. “Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu choterocho.” Komabe iye anachita khama. Iye anali wolimbikira. Chotchinga chachipembedzo sichinamuletse iye, ngakhalenso aliyense wa

iwo amene ankakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita. Iye ankadziwa mosiyana. Chinthu choyambirira, iye anali ndi chinachake mkati mwake, chimene chinamuza iye kuti iye alandira chimene iye anachipemphacho.

<sup>75</sup> Oh, anthu, usikuuno, ngati inu mungakhoze kuzisunga izo mu mtima mwanu, kuti Mulungu ali pano kuti akupatseni inu chokhumba cha mtima wanu! Ngati inu mungakwaniritse zofuna Zake, palibe chimene chidzaima.

<sup>76</sup> Pakhoza kukhala kuti panali gulu la akazi linabwera kwa iye, ndipo anati, “Taonani, Mlango Lydia,” kapena chirichonse chimene dzina lake linali, “kodi wamva kuti mwamuna wako akusiya ukapanga izi?” Sindikukaika koma kuti iye ankamukonda mwamuna wakeyo, koma iye sakanakhoza kutemberera kapena kudalitsa Icho chimene chinali mwa iye. Chinachake chinali chikunena, mwana wake wamkazi anali kufa ndi khunyu ndipo anayenera kupita kwa Yesu, ndipo, pamene iye anakafika kumeneko, chinachake chinali choti chichitika, mwamuna kapena wopanda mwamuna.

<sup>77</sup> Ena a iwo mwina ananena kuti, “Chabwino, mutani naye mwana wosautsikayu ngati izo zitalephereka?” Koma iye ankadziwa kuti izo sizikanati zilephere. Chinachake chinali mwa iye, chimene chinamuza iye kuti sizingalephereke. Ngati Iye anali konse Mulungu, Iye akanali Mulungu panobe. Izo sizingalephereke. Chotero, iye anakhalabe wolimbikira.

<sup>78</sup> Ndiye ena a iwo ayenera kuti anati: “Bwalo limene iwe ulimo, mgululo, akakuseka iwe.” Kuseka kapena kusaseka, sizinamupangitse kusintha ayi. Chinachake chinali mkati mwake! Iye anali wolimbikirabe.

<sup>79</sup> Ena a iwo akanati, “Mudzachotsedwa mu mpingo wanu.” Kuchotsedwa kapena kusachotsedwa, iye anali panjira yake, chinachake chikumukokera iye kwa Yesu! Panalibe chirichonse chimene chikanaima panjira yake, panalibe zomulepheretsa. Iye anali wolimbikira. Palibe chimene chinaima panjira yake.

Potsiriza iye anakafika kumene Iye anali.

<sup>80</sup> Anthu ambiri amaganiza, “Chifukwa chakuti iwe wafika kumene Iye ali, zonse zatheka.” Uko nkulakwitsa. Iye akhoza kubwera muno mchipinda chino usikuuno ndi kudziwonetsera Yekha wamoyo, zitatha zaka zikwi ziwiri, mwa zinthu zimene Iye analonjeza kuti akanadzachita mu tsiku lino. Iye anazichita usiku wathawu. Iye amazichita usiku uliwonse. Iye amazichita kulikonseko. Iye amatsimikizira kuti Iye akadali wamoyo. Ndipo inu mukhoza kukhala mu Kukhalapo Kwake, koma izo sindizo. Ayi, bwana. Nthawizina mumakumana ndi zovuta mukabwera mu Kukhalapo Kwake. Iye anatero.

<sup>81</sup> Pamene iye anafika, ndiye Yesu anati, Iye anali “sanatumizidwe” kwa mtundu wake. Mmodzi yemweyo amene iye anabwera akumukhulupirira, anamukana iye. Ili ndi

phunziro. Mmodzi yemweyo Uyo...Iye anali atadutsa zipata zonsezi, za chisoni ndi zokhumudwitsa, ndi chirichonse, kuti akafike kumeneko, mwa Chinachake chikututuma mkati mwa iye, chikumuuza iye kuti apite; pamene anakafika kumeneko kwa Iye, Iye anamukana iye, mosabisa. Ndipo pambali pa zimenezo, Iye anati mtundu wake sunali kanthu koma gulu la agalu. “Sikoyenera kwa Ine kuti nditenge mkate wa ana ndi kuwudyetsa iwo kwa inu agalu.”

<sup>82</sup> Bwanji ngati Iye akanati awatchule—Achipentekoste, “agalu”? Mai, sindikudziwa zomwe zikanadzachitika. Bwanji ngati Iye akanati, “Amethodisti agalu, Abaptisti agalu”? Lingaliro langa, abwerera ndikukawauza abusa kuti amalondola, panalibe kanthu kwa Munthu uyu. Koma ngati iwe unagwira, ndipo chinachake chinakugwira iwe, izo zidzakhala zosinthika.

<sup>83</sup> “Ine sindinatimizidwe kwa inu mtundu wa agalu. Sikoyenera kuti Ine nditenge mkate wa ana ndi kukupatsani inu. Ine sindinatimizidwe kwa inu. Chitsitsimutso chanu si ichi, kampani yanu sikuthandizira izi, ndipo Ine sindinatimizidwe kwa inu. Ndipo sikoyenera kwa Ine kuti nditengere nthawi Yanga pa inu, pamene inu simuli kanthu koma agalu. Ndipo nchifukwa chiyani kuti nditayire nthawi Yanga pa inu?” Chimenecho chikanakhala chokhumudwitsa chotani nanga kwa mkazi amene analibe chikhulupiriro, amene sanali atatsimikiza! Oh, ngati mpingo ukanakhoza kokha kuziwona zimenezo! Komabe iye anagwiritsitsa.

<sup>84</sup> Iye sanali a—chomera cha mnyumba chimene chimayenera kupembedzedwa, chimodzi cha izi zimene umayenera kuchita kuzipopera paliponse, inu mukudziwa, ndi kuletsa nsikidzi kwa izo. Chomera chabwino chathanzi, simumasowa kuti muzichipopera. Chomera chabwino chathanzi, kachiroombo sikangafike kwa icho, chimakhala chodzadza thanzi.

<sup>85</sup> Ndipo chikhulupiriro chabwino chobadwa kachiwiri mwa Mulungu, chikhulupiriro chenicheni cha Mzimu Woyera, palibe chimene chiti chidzakane icho. Icho sichingachite zimenezo. Icho chimakhala chakhama. Icho chikupita ku cholinga chimene Mulungu analonjeza kwa icho. Palibe chomwe chiti chidzakane icho. Icho chikupita mulimonse. Inde, iye sanali wa haibridi.

<sup>86</sup> Lero, zonse zomwe tiri nazo ndi haibridi. Inu mukambe za chimanga cha haibridi, ine ndimachiwona icho uko pa zikwangwani kuno. Icho si chabwino. Icho chikupha anthu. Tayang’anani pa *Reader’s Digest*, anati, “Ngati akazi apitirize kumadya, chiti chidzachitike ndi chiyani, iwo samadzakhalanso ndi ana awo, mu zaka twente kuchokera pano. Iwo samadzakhozanso kubereka ana awo.” Iyo ikuphwasula izo, mpaka khansa yatenga malo. Oh, chirichonse, chinthu

chonsecho chadyedwa ndi mphutsi. Kusakhazikika kumeneko kwagwetsera zasayansi, pa kusinthikako, pansi.

<sup>87</sup> Yesu anati, Mulungu anati, pachiyambi, “Mulole mbewu iliyonse ibale mwa mtundu wake.” Inu mutenge chimanga cha haibridi, ndipo muchipange haibridi icho, ndi kuchibzala icho; mudzabzale mbewu yomweyo chaka chamawa, inu simudzapeza kalikonse. Inu mudzakhala ndi mbewu yowoneka bwino, koma mulibe kalikonse. Iwo apanga haibridi chirichonse, mdzikoli.

<sup>88</sup> Inu mumutenge bulu; ndi, kapena mutenge a—jack ndi kumupangitsa haibridi kwa kavalo, inu mudzakhala ndi bulu, koma bulu ameneyo sadzakhoza kudzibalanso yekha. Iye ndi chinthu chaumbuli kwambiri padziko lapansi. Ine ndawayendetsapo iwo, mmoyo wanga wonse kuno, inu mudza... iye adzadikirira mpaka miniti yotsiriza yakufa, kuti akukankheni inu. Iye samadziwa kanthu. Inu simungamuphunzitse iye kalikonse.

<sup>89</sup> Mukayankhula naye iye, iye amangokhala monga ochuluka a otchedwa Akhristu omwe amakhala ndi makutu ataimirira, “Hoho? Hoho?” Iwo samatero nkomwe... Kulira, ndipo samadziwa zomwe akulirazo. “Masiku a zozizwitsa anapita. Kulibeko chinthu chotero chonga machiritso.” Koma inu mutenge ubwino... Iye samadziwa komwe anachokerako. Iye sakudziwa kuti abambo kapena amayi ndi ndani.

<sup>90</sup> Koma kavalo weniweni amadziwa yemwe anali abambo ake, omwe amayi ake anali, omwe agogo ake anali, agogo-aamuna, agogo-agogo-agogo-agogo-, njira yonse kubwerera mmbuyo. Iye amadziwa kumene iye anachokerako.

<sup>91</sup> Chomwechonso Mkhristu weniweni wobadwa kachiwiri amadziwa kumene iye anachokerako. Chiyambi chake sichinali ndi John Wesley, Luther, kapena winawakenso. Izo zinayambira pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mulungu Mwiniwake anabwera pakati pa anthu Ake. Ndipo Iye ndi Mawu akuwonetseredwa. Inu mukhoza kumuza iye Mawu, ndipo iye adzanena kuti, “Ameni!”

<sup>92</sup> Winayo adzati, “Ine sindikudziwa za Zimenezo.” Mukumuwona bulu ameneyo, haibridi? Mwaona, iye samadziwa kumene iye akupita, iye samadziwa kumene anachokerako. Iye ali mmawonekedwe oipa.

<sup>93</sup> Mkazi ameneyo sanali wa mtundu umenewo. Iye sanali chomera cha haibridi. Iye anali atagwira chinachake. Inu simumasowa kuti mumupembedzere iye ndi kumupopera iye, ndikuti, “Tsopano, wokonedwa, chonde, tsopano ndirole ndikupemphe iwe. Iwe uyenera kutsikira kuno.” Ayi, bwana. Panalibepo. Chirichonse kuyesera kumulepheretsa iye.

<sup>94</sup> Mkhristu weniweni amamenyera malo ake. Iye amayenera kuti ayime yekha, iyeyo ndi Mulungu, ndipo iye amamenyera

inchi iliyonse ya malowo, chotero inu simumasowa kuti muchite kuwapembedzera iwo pamenepo.

<sup>95</sup> Ndiro lomwe liri vuto ndi mpingo wa Chipentekoste lero, ife tiri nawo makanda Achipentekoste omwe angowazidwa kumene ndi kufairidwa *ichi* ndi *icho*, ndi *chinacho*, mpaka zathera kukhala gulu la ma haibridi. Chimene tikuchisowa lero ndi kuyeretsa m'nyumba, kuchokera pa guwa mpaka kwa—woyang'anira nyumba, ndi kuyambiranso, ndi kupeza chikhulupiriro chenicheni chobadwira mwa anthu. Eya.

<sup>96</sup> Ayi, iye sanali wa haibridi, munga otchedwa mbewu ya okhulupirira ali lero. Kodi iye anachita chiyani? Iye anavomereza kuti Iye anali kulondola, Mawu.

<sup>97</sup> Ndipo chikhulupiriro nthawizonse chimavomereza kuti Mawu ndi olondola. Amen. Ngati chikhulupiriro chanu sichivomereza Mawu aliwonse a Mawu a Mulungu, ndi *ameni*, pali chinachake cholakwika ndi chokuchitikirani chanucho. Baibulo linati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ngati izo sizikunena *ameni* kwa zimenezo, ndiye kuti pali chinachake cholakwika. Yesu anati, "Ntchito zimene Ine ndikuchita inunso mudzazichita." Ngati izo sizikunena *ameni* kwa izo, ndiye pali chinachake cholakwika. Ngati izo zizingavomereze Mawu aliwonse a lonjezo la Mulungu, ndi *ameni*, pali chinachake cholakwika.

<sup>98</sup> Iye anavomereza kuti Iye amanena zoon. Anavomereza kuti sanali kanthu koma galu. Koma ankangotsatira zinyenyiswa.

<sup>99</sup> Sitingakhale ife. Oh, ayi. Ife tiyenera kukhazikidwa pampano, ndipo, "Ngati sanditumikira ine usiku woyamba, ine sindibwererako usiku wotsatira."

<sup>100</sup> Tsopano, mukuona, oh, iye anali wosiyana bwanji. Kukaikidwa kumbuyo, ndi kukankhidwira mmbuyo, kukankhidwira kunja, kuyikidwa panja, chirichonse chomwe chinali, iye anali atatsimikiza. Iye anali wakhama, wolimbikira. Chinachake mkati mwake, chinamuza iye kuti achipeza icho mosalabadira kuti adikirira nthawi yotalika bwanji, zomwe ankayenera kudutsamo. Iye adzachipeza icho mulimonse. Iye ankafuna zinyenyewazo. Sankafuna chakudya chamadzulo chathunthu. Iye anati, "Agalu amadya zinyenyiswa za pansu pa gome la mbuye."

<sup>101</sup> Ndiyo njira yake yochitira izo. Osatenga mpando wapamwamba; kumatenga mpando wakumbuyo. Osamatero. . . Ingokhalani munthu wamng'ono. Njira yopitira mmwamba ndi pansu, nthawizonse. "Iye amene adzichepetsa yekha adzakwedwa. Iye amene adzikweza yekha adzatsitsidwa." Njira yopitira mmwamba ndi pansu, nthawizonse.

<sup>102</sup> Kumbukirani, iye anali asanawonepo chozizwitsa. Iye anali Wamitundu, koma anali ndi chikhulupiriro.

<sup>103</sup> Iye anali chinachake chonga hule, Rahabi. Ananena kwa azondi. . . Iye sananene kuti, “Dikirani mpaka ine ndidzawone momwe Yoswa amapesera tsitsi lake. Bwanji, kodi ankhondo anu onse amawoneka bwanji? Kapena amagwiritsa ntchito malupanga otani? Kodi ndi zida zotani? Nkhondo yamtundu wanji?” Iye anati, “Ndamva kuti Mulungu ali ndi inu. Izo nzabwino mokwanira kwa ine. Ine ndikufuna chifundo.” Iye anakhulupirira.

“Chikhulupiriro chimadza pakumva, ndipo pakumva Mawu a Mulungu.”

<sup>104</sup> Penyani, “Kwa maneno awa, chifukwa cha maneno awa,” Yesu anati, chifukwa iye anachita khama, ndi kubwera.

<sup>105</sup> Tsopano, poyamba, anamutchula Iye, “Mwana wa Davide.” Tsopano ngati. . . Iye anali, monga Wamitundu, analibe chodzinerera pa Iye ngati Mwana wa Davide. Koma pamene iye anati, “Ambuye,” Iye anali Ambuye wake, koma osati Mwana wa Davide, kwa izo.

<sup>106</sup> Anali ndi mafikidwe olondola kwa mphatso ya Mulungu. Ndipo ndiyo njira yokhayo yolandirira chirichonse, ndi kubwera ndi mafikidwe olondola. Iye anali Wamitundu woyamba yemwe chozizwitsa chinayamba chachitidwapo. Chikhulupiriro chimavomereza kuti Mawu ndi olondola, ndi odzichepetsa ndi olemekeza. Ndi chimodzimodzi lero, muzikhala ololera kutengapo gawo, kulikonseko, “kuti ndikafike kumeneko.”

<sup>107</sup> Kodi inu munayamba mwazindikirapo Marita, mu Kukhalapo kwa Yesu, anali wakhama? Marita, pamene iye anatulukira, ngakhale iye anali ndi mchimwene amene ankamukonda Iye, ngakhale iye anali atatsegula nyumba yake ndi kuchisiya tchalitchi, ndi zina zotero, ndipo Lazaro ndi Iye anali abwenzi; ndipo Lazaro anali atafa, mmanda, ndipo anali ali mmenemo kwa masiku anai, akuipiraipira kale. Mphuno inali itagwera mkati, mnofu unali mmafupa ake. Iye anali wakufa.

<sup>108</sup> Ine ndinali kuyankhula ndi mkazi wa chikhulupiriro china amene samakhulupirira kuti Iye sanalinso kuposa mneneri chabe kapena munthu wabwino.

<sup>109</sup> Ine ndivomereza kuti Iye anali mneneri. Koma, Iye anali woposa mneneri, Iye anali Mulungu wa aneneri. Iye anali chonse chimene aneneri anali, zinali mwa Iye, kuphatikizapo Mulungu, ndipo zonse za izo pamodzi zinamupanga Iye.

<sup>110</sup> Ife tinali tikupita kumusi, usiku wina, iye anati, “Ngati nditatsimikizira kwa inu, Bambo Branham!” Anati, “Ine ndangokhala ndi cholakwika chimodzi ndi Uthenga wanu.”

Ine ndinati, “Ine ndikuyembekeza Ambuye ali nacho, ali ndi cholakwika chimodzi chokha, angandipeze nacho.”

111 Anati, “Mumabwekerera kwambiri za Yesu.” Anati, “Inu—inu mumamupanga Iye Mulungu.”

112 Ine ndinati, “Iye anali Mulungu. Ngati Iye sanali Mulungu, Iye anali wonyenga wamkulu yemwe dziko linayamba lakhalapo naye.”

Iye anati, “Inu mumamupanga Iye Waumulungu.”

Ine ndinati, “Iye anali Waumulungu.”

“Oh,” anati, “Iye anali—Iye anali munthu wabwino.”

113 Ine ndinati, “Iye anali woposa munthu wabwino. Iye anali Mulungu. Iye anali Waumulungu.”

Anati, “Ine nditsimikizira kwa inu, ndi Baibulo lanu lomwe, Iye sanali Waumulungu.”

Ine ndinati, “Mungachite bwanji zimenezo?”

114 Iye anati, “Mu Yohane Woyera, mutu wa 11, pamene Yesu anapita kumanda, kuti akamuwukitse Lazaro, Baibulo linati, ‘Iye analira.’”

Ndipo ine ndinati, “Kodi limenelo ndi Lemba lanu?” Ine ndinati . . .

“Inde.”

Ine ndinati, “Inu mwalephera . . .”

Anati, “Iye anakhoza bwanji kulira ndi kukhala Waumulungu?”

115 Ine ndinati, “Iye anali ziwiri zonse munthu ndi Mulungu. Ameneyo anali munthu amene ankali layo, ndithudi. Ine ndikuvomereza kuti ameneyo nali munthu akulira. Koma pamene Iye anadzayima pambali pa manda, anadziwongola thupi Lake laling’ono lofooka, ndipo anati, ‘Lazaro, tuluka,’ ndipo munthu amene anali atafa, masiku anai, anayima pa mapazi ake nakhalanso ndi moyo, ameneyo anali woposa munthu.” Inde, bwana.

116 Chivundi chinamudziwa mbuye wake. Solo inamudziwa Mlengi wake. Ndipo iye anali ulendo wa masiku anayi kwinkwake; ine sindikudziwa, inunso simukudziwa. Koma, mulimonse, pamene Iye anayankhula, iye anatulukira. Ameni. Zimenezo zinali woposa munthu.

117 Iye anali munthu pamene Iye ankatsika kuchokera pa phiri, usiku umenewo, Iye atatha kubwera, ali wanjala; akutsika akuyang’ana pamitengo, kuti apeze chinachake choti adye, akuyang’ana pa mtengo, pamene Iye anawutemberera mtengo umene unalibe chipatso. Iye anali munthu pamene Iye anali ndi njala. Koma pamene Iye anatenga mabisiketi asanu ndi nsomba ziwiri, nadyetsa makwi zisanu, natolera mitanga isanu ndi iwiri yodzadza ndi makombo otsala, ameneyo anali woposa munthu. Ndi zimenezotu.

118 Iye anali munthu pamene Iye anagona kunja uko pa madzi usiku umenewo, kumbuyo kwa ngalawa. Ukoma unali utachoka mwa Iye, utali wa tsiku lonse, akulalikira, ndi kuchiritsa odwala; ukoma ukuchoka mwa Iye, kuchokera kwa anthu, kuzindikira malingaliro mu mtima mwawo. Ndipo ziwanda teni sauzande za m'nyanja zinalumbira kuti zimumiza Iye usiku umenewo. Sitima yapamadzi yaing'ono yakale ija ngati choyingira botolo kunja uko, ikuyandama mmwamba-ndi-pansi. Mdierekezi anati, "Ine ndamupeza Iye tsopano." Ndipo izo zinkawoneka ngati zonse zatha. Koma pamene Iye kamodzi anadzuka, anabwera ndipo anadzayika phazi Lake pa chingwe cha ngalawa, ndipo anayang'ana mmwamba ndipo anati, "Bata, pakhale mtendere," ndipo mphepo ndi mafunde zinamumvera Iye, ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu.

119 Iye anali munthu pamene Iye anafuulira chifundo, pa mtanda, zoono. Pamene Iye anafuula kufuna chakumwa ndipo anamupatsa Iye vinyo wosasa, ameneyo anali munthu. Pamene Iye anafa, akuwukha magazi, akulira, akupachikidwa, akukhomeredwa pa mtanda, Iye anali munthu. Koma mmawa wa Isitala pamene Iye anamatula zisindikizo za manda naukanso kachiwiri, ndipo anati, "Ine ndine Iye amene ndinali wakufa, ndipo wamoyo kwanthawizonse," ameneyo anali woposa munthu. Ameneyo anali Mulungu mwa munthu, Mwana Wake.

120 Nzosadabwitsa, Marita ndi kumvetsa uku, iye anali wolimbikira mu Kukhalapo kwa Yesu. Anati, "Ngati Inu mukadakhala kuno m'bale wanga sibwenzi atafa. Koma ngakhale tsopano, chirichonse chimene Inu mudzampempha Mulungu, Mulungu adzapereka icho kwa Inu."

121 Oh, ngati ife tikanangotengera mawu amenewo mmitima yathu usikuuno! "Ine ndikudziwa kuti ndikukhala pa chikuku. Ine ndikudziwa ine ndiri ndi khansa, ndiri ndi vuto la mtima, chirichonse chimene icho chiri. Ine ndikudziwa adokotala akuti ola langa lomaliza layandikira. Koma ngakhale tsopano, Ambuye!" Chirichonse chimene mungamupemphe Mulungu, Iye adzachichita icho. Ndipo Iye akukhala pa dzanja lamanja la Ukulu Wake, kuti azitetezera pa kuvomereza kwathu. Mungokhala wakhama monga Marita anali.

122 Zinkawoneka ngati Iye anamukana iye. Anantumira Iye, ndipo Iye sanapite. Anantumiranso, ndipo Iye sanapite. Potsiriza, atatha kuikidwa mmanda, masiku anai, ndi Uyu apa. Koma anakhalabe wakhama. Iye anali atagwira chinachake. Iye anali atawona ntchito Zake ndipo iye anadziwa kuti ameneyo anali Mulungu. Iye ankadziwa kuti izo zinali. Iye anali wakhama. Iye anali atapeza zomwe anapempha.

123 Mkazi wa ku Shunemu, pamaso pa Eliya, anali wakhama. Oh, mwanayo anali atafa, ndipo atagona pa kama wake.

Ndipo Eliya anayesa kutenga ndodo yodzozedwayo ndi kuitumiza, ndi Gehazi, kuti akaigoneke pa mwanayo. Koma chikhulupiriro chake sichinali mu ndodoyo, icho chinali mwa mneneri. Iye ankadziwa kuti Mulungu anali mwa mneneri ameneyo, pakuti iye anali atawawona mawu amene iye ananena akukwaniritsidwa. Iye anali mneneri wotsimikiziridwa, ndipo iye ankadziwa kuti zimene iye amanena zimachokera kwa Mulungu. Ndipo iye anati, “Pali moyo wanu, ine sindidzakusiyani inu mpaka nditapeza chifukwa chake.” Ndipo anakhala ndi iye. Anali wakhama mpaka iye anapeza zomwe anapempha.

<sup>124</sup> Izo zikundikumbutsa ine, kuno osati kale kwambiri, mkazi wamng’ono akubwera kuchokera ku California, pamene ine ndinali kukhalabe mu Jeffersonville. Zakhala pafupifupi zaka zitatu kapena zinayi zapitazo. Iye anali ndi chotupa, ndipo chotupa chokhacho chinali cholemera mapaundi fifite. Iwo ankachita kumunyamula polowa naye mnyumba, ankamukhazika iye kumbuyo. Iwo...Iye ankadziwa kuti ine ndikakhala kumeneko usiku umenowo. Iye ankaganiza kuti ine ndipempherera odwala. Koma ndinangobwera kuti ndidzayankhule kwa omvetsera, mwinamwake za zomwe ife tiri nazo muno usikuuno. Pambuyo pomaliza kuyankhula... Ena a iwo anali atamuza iye, “Iye samapempherera odwala usikuuno.”

<sup>125</sup> Koma iye ankafuna kuti apemphereredwe, iye ananena mu mtima mwake, ndipo anakhulupirira. Iye anayamba wakhalapo mu msonkhano, ndipo anati, “Ine ndikukhulupirira ngati M’bale Branham angandipempherere ine, ine ndichiritsidwa.” Ndipo usiku umenowo, awiri kapena atatu a madikoni anamudutsa iye pamenepo, ndipo anapita panja kumbali pa nyu-...nyumbayo, ndinabwera pamenepo kumbuyo, ndinadzamugoneka iye pakhomo.

<sup>126</sup> Ndipo ndinayamba kuyenda ndi Billy Paul, kudzera kumbuyo. Iye anadzandigwira mwendo wa thalauza, monga *choncho*. Iye anati, “M’bale Branham,” iye anati, “Nthawizonse ndakhala ndikukhulupirira kuti ngati mutapempha Mulungu, Mulungu adzandichiritsa ine.”

<sup>127</sup> Ine ndinayika dzanja langa pa iye, ndinati, “Ndiye, mlongo, malingana ndi chikhulupiriro chanu, zikhale izo kwa inu.”

<sup>128</sup> Miyezi ingapo zitachitika izi, ine ndinakumana naye mu a—msonkhano kumeneko. Apo iye anali, atayima ndi chiuno changwirowo. Chotupa cha mapaundi fifite chinali chitapita. Iye anati, “Ndimutengera mkazi aliyense muno mchipinda chovalira, ndipo ndikumulola iye awone ngati pali chipsyera pa ine paliponse. Chithunzi changa ndi *ichi* chimene ndinali.”

<sup>129</sup> Chinali chiyani chimenecho? Kaya umapempherera odwala kapena ayi, iye anali wakhama. Iye anali atabwera kuchokera

ku California, kuti adzachiritsidwe, ndipo sanali kubwerera mwanjira ina iliyonse koma kuchiritsidwa. Iye anali wakhama.

<sup>130</sup> Ndikukumbukira ndikuitanidwa pafupi ndi bedi la mnyamata yemwe anali kumwalira, kuno zaka zingapo zapitazo, ndi diphtheria yakuda. Ndipo iwo samandilola ine kupita mmenemo, chifukwa ndinali ndi ana. Adokotala anati, “Simungathe kukalowa mmenemo, ndinu bambo wokwatira.”

<sup>131</sup> Ine ndimadziwa kuti anali Mkatolika, ndipo ndinati, “Ngati—ngati mnyamatayo akanakhala Mkatolika, kodi mukadamulola wansembe kuti alowe mmenemo?”

Iye anati, “Eya, koma iye—iye ndi wosakwatira.”

Ine ndinati, “Iye amayendera ana, ndi zina zotero.”

Anati, “Sindiro funsolo, Bambo Branham.”

<sup>132</sup> Ine ndinati, “Mukanamulola wansembe kulowa ndi kumupatsa iye miyambo yomaliza. Iyi ndi miyambo yomaliza. Mnyamatayo akufa. Ndiloleni ndikafike kwa iye.”

<sup>133</sup> Chabwino, potsiriza ndinamunyengerera iye. Ndipo iye anandiveka ine ngati Ku Klux Klan, kapena chinachake, mitundu yonse ya zinthu paliponse.

<sup>134</sup> Ndipo amayi okalamba ndi abambo anali atayima pamenepo. Ndinali nditasiya msonkhano, ndipo—bambo ndi mayi okalamba anati, “Ngati mungabwere kudzapemphera, mwana wanga adzakhala moyo.” Mnyamatayo anali pafupifupi zaka seventini, eyitini zakubadwa. Ndinali ndi cardiogram, makina pamenepo, a mtundu wina. Anakhala ali chikomokere kwa masiku awiri kapena atatu, ndipo sankadziwa kanthu. Amayiwo ndi abambo anandilandira ine pamene ndimalowa. Ndinagwada pansi ndipo ndinapemphera kapemphero kakang’ono ka chikhulupiriro.

Ine ndinati, “Bwana, kodi inu mumamukhulupirira Mulungu?”

<sup>135</sup> Iye anati, “Ndi mtima wanga wonse, chinthu chokhacho chimene ine ndikufuna kuti inu muchite ndi kumupempha Mulungu. Mulungu apereka icho.”

<sup>136</sup> Ine ndinati, “Zikomo inu, m’bale, chifukwa cha chidaliro chanu. Mulole ine ndisadzazipachike konse zimenezo.”

<sup>137</sup> Ine ndinadzayika manja pa mwana wamng’ono, ndipo ndinapemphera, “Ambuye Yesu, mulole chikhulupiriro cha abambo ndi amayi awa chilumikizane ndi changa, ndi kubwera pamaso pa mpandowachifumu Wanu usikuuno. Mulole mnyamata uyu akhale ndi moyo ndipo asafe, chifukwa tikukhulupirira. Mu Dzina la Yesu.”

<sup>138</sup> Tinanyamukapo. Ndipo abambo anafikira nawagwira amayiwo pa mapapo akale achitsulo, a chinthu chimene iye anali kupumira pamenepo, ndipo anati, “Amayi, kodi izi

sizodabwitsa? Kodi izi sizodabwitsa? Oh, ndi zodabwitsa kwambiri!”

<sup>139</sup> Ndipo namwino wamng’ono ameneyo atayima pamenepo, iye anadabwitsidwa. Chipewa chaching’ono chija chinakhala ngati chikugwa kuchokera pamutu pake. Iye anayang’ana pozungulira, ndipo anati, “Bwana, sindikumvetsa. Inu mungakhoze bwanji kuchita chonchija, inu ndi mkazi wanu, ndi mwana wanu wamwamuna akufa?”

Iye anati, “Wokonedwa, mwana wanga sakufa.”

<sup>140</sup> “Chabwino,” anati, “adokotala ananena kuti akufa.” Anati, “Kuti,” chirichonse chomwe makinawo anali, anati, “pamene mtima ukutsika motsika chomwecho, ndi malungo awa, izo sizinayambe zadziwikapo, mu mbiriyakale, kuti zinabwererapo konse.”

<sup>141</sup> Inu sindidzaiwala konse chikhulupiro cha mbadwa yakale ija. Iye anali wa, ine ndikukhulupirira, gulu la A. B. Simpson. Anayenda chokwera ndipo anadzayika manja ake pa mapewa, iye anali pafupifupi usinkhu wa zaka sikisite, anadzayika manja ake pa mapewa a mtsikana wamng’ono uyu, anamuyang’ana iye mu nkhope. Iye anati, “Wokonedwa, iwe ukuyang’ana pa makinawo. Ndizo zonse zomwe ukudziwa kuti uyang’ane. Koma ine ndikuyang’ana pa lonjezo, limene Mulungu anati Iye akanadzachita izo.”

<sup>142</sup> Zimatengera zomwe mukuyang’anapo. Iwo anali akukumbatirana wina ndi mzake, ndipo akusangalala pamenepo, m’bale. Ndipo iye ndi wokwatira, ndiponso mmishonare mu Africa tsopano, ali ndi ana awiri. Chifukwa chiyani? Chifukwa bambo ndi mayi amatha kupirira nthawi ya mdima kwambiri. Khama! Inde, bwana, khama! Khalani ndi chikhulupiro mwa Mulungu!

<sup>143</sup> Mikaya wamng’ono, pamaso pa aneneri ophunzitsidwa foro handiredi amenewo, anali wakhama pamene anali ndi masomphenya ochokera kwa Mulungu. Ngakhale iwo...Iye anali wosiyana. Iwo anakomana naye iye ndipo anamuuza iye, “Tsopano tikubwezeretsa iwe mu mgwirizano ngati unene chinthu chomwecho, iwe, chimene iwo anena.”

<sup>144</sup> Iye anati, “Pali Ambuye, ine ndingonena zomwe Iye andiuze kuti ndinene.” Ndipo masomphenya ake anayesedwa ndi Mawu a Mulungu, ndipo ananena uneneri wake, mulimonse.

<sup>145</sup> Iwo anati, “Tikamuponyera iye m’chipinda chamkati, ndi kumpatsa iye chisoni, mkate wachisoni, ndi madzi achisoni.” “Ndipo pamene amabwerera,” iye anati adzachita naye iye, Ahabu anatero.

<sup>146</sup> Iye anati, “Ngati mungabwerere konse, Mulungu sanayankhule ndi ine.” Iye anali wakhama. Iye ankadziwa pamene iye amayima.

147 Munthu wakhungu amene anachiritsidwa ndi Yesu sanathe kutsutsana ndi fioloje yawo. Iwo anati, “Ndani anatsegula maso ako?”

Iye anati, “Munthu wotchedwa Yesu wa ku Nazarete.”

148 Anati, “Munthu uyu ndi wochimwa. Ife sitikudziwa kumene Iye anachokerako.”

149 Tsopano, anawapatsa iwo yankho labwino. Iye anati, “Inu ndinu atogoleri achipembedzo a tsiku lino. Ndipo Munthu uyu wandipatsa ine kupenya kwanga, ndipo komabe inu simukudziwa kumene Iye anachokera.” Iye anali ndi fioloje yabwino yokongola yakeyake. Sanathe kutsutsana nawo iwo. Koma iye ankadziwa chinthu chimodzi, iye amakhoza kupenya. Ndipo samachita manyazi. Bambo ake ndi amake anachita manyazi kunena chinachake cha izo, koma osati iye. Iye anali ataziwona izo. Iye anali atazimverera izo. Iye anali ndi zotsatira za izo. Chinachake chinali chitamuuza iye, ndipo iye anali wakhama.

150 Filipino, mwamsanga pamene iye anawona, phunziro la usiku wathawu, chiyani, pamene anabwera mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, pamene anamuwona wa Simoni. . . kapena mchimwene wake wa Andrey. Fili- . . .

151 Petro anabwera mu Kukhalapo, yemwe anali Simoni pamenepo, anabwera mu Kukhalapo kwa Yesu. Simoni anali ataphunzitsidwa, ali mwana, kuti Mesiya adzakhala mneneri. Pamene iye anayenda kupita mu Kukhalapo Kwake, ndipo Iye anamuza iye, “Dzina lako ndiwe Simoni ndipo ndiwe mwana wa Yonasi.” Iye anali wakhama. Iye anali atakonzeka pamenepo. Anadzakhala mutu wa mpingo.

152 Pamene Filipino anachiwona Icho, iye anamudziwa wowerenga Baibulo wina wabwino yemwe ankadziwa Choonadi. Anali wakhama. Iye anazungulira phirilo ndipo anakamutenga iye.

153 Ndipo pamene Nataniele anabwera, mwamuna wodziwika, Mhebri weniweni, mwamuna, Mhebri wokhazikika, munthu wabwino kwenikweni, waluntha bwino, iye anali munthu wopambana. Koma pamaso pa wansembe wake ndi pamaso pa aliyense wa iwo, pamene Yesu anamuyang’ana iye ndikuti “taonani wa Chiisraeli amene mwa iye mulibemo chinyengo,” iye anati, “Rabi, Inu munandidziwa bwanji ine? Ine sindinayambe ndakuwonanipo Inu kale. Inu munadziwa bwanji yemwe ine ndinali?”

154 Iye anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.”

155 Iye anagwa pa mapazi Ake, ndipo anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo. Inu ndinu Mfumu ya Israeli.” Chifukwa chiyani? Anali wakhama mosalabadira kanthu

za zomwe wina aliyense ankaganiza. Iye anali atakumana nacho Chinthu chimene iye anali atachiwerenga. Zimene ankayembekezera kuzipeza mwa Yesu, anali atazipeza.

<sup>156</sup> Mkazi wamng'ono wachiwerewere anabwera ku chitsime, tsiku lina, kuti adzatunge madzi. Pamenepo panakhala Yesu, Munthu wamba atavala zovala wamba, akudya chakudya wamba, akuyankhula chinenero cha anthu wamba, basi chinenero wamba cha mu msewu monga momwe aliyense amayankhulira. Ndipo iye anayankhula kwa Iye; Iye anayankhula naye. Iye anapeza pamene vuto lake linali, ndipo Iye anati, "Pita ukamtenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno."

Iye anati, "Ine ndiribe mwamuna."

<sup>157</sup> Anati, "Iwe wanena bwino. Wakhalapo nawo asanu, ndipo amene ukukhala naye tsopano si wako." Mwamsanga mbewu yokonedweratu imeneyo mu mtima mwake inakhudza Moyo!

<sup>158</sup> Pamene Icho chinawakhudza Afarisi, Icho chinangotembuzira chinthu chonsecho kukhala chakuda. Iwo anati, "Munthu uyu ndi Bezebeule. Iye ndi wambwebwe."

<sup>159</sup> Koma iye anadziwa kuti Mawu anali "akuthwa, amphamvu kwambiri kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndi Wozindikira maganizo a mu mtima."

<sup>160</sup> Iye anati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Ife sitinakhale naye wina kwa zaka mazana anayi. Ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri. Koma ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzadza, Iye adzatiuza ife zinthu izi."

<sup>161</sup> Iye anati, "Ine ndine Iye amene akuyankhula ndi iwe." Ndithudi Amene anachita chozizwitsa sanganene bodza. Iye anali Mneneri. Iye . . . Iye anati, "Ine ndine Mesiya ameneyo. Ine ndine Mmodzi, amene akuyankhula ndi iwe. Ndine Iye."

<sup>162</sup> Tsopano kuyesera kumuletsa iye? Ngati wina anakhalapo Kummawa, inu mukudziwa, mwamuna mu msewu sakanamumvetsera hule. Iye analibe liwu nkomwe. Koma kuyesera kumuletsa iye, monga nyumba yoyaka moto pa tsiku lamphepo, simungathe kuchita zimenezo. Mpaka ku msewu iye anapita, akukuwa, "Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya yemwe? Ndi Uyo wakhala uko pa chitsime tsopano. Ameneyo ndi Mesiya yemwe. Ife tamuyembekezera Munthu ameneyo kuti adzabwera, ndipo ndi Uyo wakhala apoyo. Iye wandiuza ine zinthu izi." Baibulo linanena kuti anthu anakhulupirira chifukwa cha umboni wa mkaziyo.

<sup>163</sup> Potseka, ine ndikhoza kunena. Ine ndikuwona anthu ena achi Spanish akhala pano, ine ndikhoza kunena izi. Ine ndinali ku Mexico yakale, osati kale kwambiri, ku-kubwalo kumusi uko, mtundu wina wa malo. Ife timalephera kulowa m'bwalo la

ng'ombe, kapena chimkombero chachikulu, koma tinapeza malo kumeneko kumene anthu zikwi zingapo anasonkhana. M'bale Espinoza, ine ndikuganiza m'bale wa Assembly of God, inu nonse mukumudziwa iye, wochokera ku California. Iye anali wondimasulira wanga.

<sup>164</sup> Usiku zisanachitike zimenezo, panali bambo wakhungu wokalamba anabwera pa nsanja, yemwe samakhoza kupenya nkomwe. Ine ndinayang'ana pa iye. Ndinavala nsapato zabwino, ndi zovala zabwino. Bambo wokalamba wosauka, wokwiya, thalauza lonse litang'ambika, chipewa chake chakale chosokedwa nacho—ndi, ankawoneka ngati, chingwe chomangira. Ndipo iye anali wakhungu; ndevu zoyera zikulendewera pansu. Mapazi ake akale, aakulu akale, ndipo mwinamwake anali asanavale nsapato, kwa zaka. Fumbi paliponse. Wakhungu kwathunthu. Ine ndinayang'ana pa iye. Ine ndinaganiza, “Abambo anga akanakhala pafupifupi zaka zimenezo, ngati akadakhala ali moyo.”

<sup>165</sup> Ine ndinazembera kwa iye. Ndinati, “Inu muli bwanji?” M'bale Espinoza anamasulira.

<sup>166</sup> Ine ndinakhazika phazi langa mmwamba pambali pa lake, kuti ndifufuze. Panali kansalu kakang'ono kudutsa nsanjayo kotambalala pafupifupi kuchulukitsa kanayi kapena kasanu kuposa iyi. Ndinaganiza, “Ngati nsapato zanga zimukwane, ine ndimupatsa nsapato zanga.” Oh, mapazi ake anali aakulu kuposa anga. Ine ndinakweza mapewa anga mogundana naye, ngati kuti ndimukumbatira iye, mapewa ake anali otambalala kuposa anga. Ine ndinawona ndiye kuti sindingathe kumupatsa malaya anga. Ine ndinaganiza, “Mulungu, kodi ndichite chiyani? Munthu wokalamba wosauka, mwinamwake sanadyepo chakudya chabwino mmoyo wake.” Ndipo iye anali pamene, akudya mimbulu yotaidwa kumusi uko kwina; koma amayenera kuwononga ndalama zochepa zomwe anali nazo, kuti akagule kandulo yamafuta, kuti akaiyatse iyo pa guwa la golide la madola—millioni, chifukwa cha machimo ake, kumakhala mu zikhulupiriro zoterozo ndi mdima wonga umenewo! Ine ndinaganiza, “Ndi nthawi bwanji! Kodi choikidwiratucho chingakhale choyipa bwanji?”

<sup>167</sup> Ine ndinakumbatira nkono wanga pa iye, ndipo ndinalira, “O Mulungu, muchitireni iye chifundo!”

<sup>168</sup> Iye anakuwa, “Gloria a Dios!” Ndipo pafupifupi nthawi imeneyo ine ndinayang'ana pozungulira, iye amakhoza kuwona mwabwino momwe ine ndikanathera, akudutsa pa nsanja.

<sup>169</sup> Ndipo a—usiku wotsatira pamene ife timabwera mmenemo, munali mulu wa zovala zakale ndi mashawelo, ndi zipewa, kukwera mmwamba mapazi atatu kapena anai, monga *chonchi*, njira yonse kudutsa pamene. Iwo ankadziwa bwanji kuti ichi ndi cha ndani? Inu mukuganiza kuti amasamala? Iwo

anabwera ku tchalitchi mmawa umenewo pa eyiti kapena naini koloko, popanda mipando yoti akhalemo; kunjā uko, ndipo iyo ikuvumba mvula, ndipo akungotsamirana wina ndi mzake. Akazi ali ndi tsitsi lawo lonse likulendewera pansi, ndipo atawagwirizira ana ndi zinthu. Mvula ikuvumba pansi, inabwera naini koloko, ndipo ine sindikadakhala kumeneko mpaka pafupi hafu pasiti eyiti kapena naini usiku umenewo. Iwo amafuna kukhala otsimikiza kuti akakhala kumeneko. Anayima pamenepo akudikirira mpaka nditalowa.

<sup>170</sup> Iwo ananditsitsira ine pansi kuchokera pa makwerero a chingwe, kumbuyo kwa bwalolo, pamene ine ndinadzera pobwera mkatimo monga *chonchi*, ndinayenda kupita pa nsanja. Billy Paul... Ndipo munthu amene ndinamutcha kuti *Mañana*, kutanthauza “mawa,” iye nthawizonse amakhala wochedwa kubwera kudzanditenga ine. Ndiye chotero ndinati, “Ingobwerani mawa, inu mwawononga usikuuno.” Chotero iye ananditengera ine kumeneko ndipo ananditsitsira ine pansi, ndipo ndinadzabwera pa nsanja.

<sup>171</sup> M’bale Jack Moore, ambiri a inu mukumudziwa iye, kutsidya kuno ku Shreveport, iye anali ndi ine; ndi M’bale Espinoza ndi angapo a abale. Ndiye pamene ife tinali titayima pamenepo pa nsanja, Billy anabwera. Ine ndinamva kuti kuli chipwirikiti chachikulu, kutali uko, uko kunali zikwi kuchulukitsa zikwi atakhala mmenemo.

<sup>172</sup> Billy anati, “Adadi muyenera kuchitapo kanthu. Mkazi wamng’ono wachi Spanish cha kuno,” anati, “ali ndi mwana wakufa m’manja mwake.” Anati, “Mwana ameneyo wamwalira m’mawa uno, akutero, molawirira. Ndipo—ndipo Mañana anapereka makadi apemphero amenewo, ndipo,” anati, “ndipo iye alibe khadi la pemphero, ndipo ine ndiribe limodzi.” Anati, “Ndipo iye watsimikiza kuti amubweretsa mwana ameneyo mu mzere wa pemphero.” Anati, “Ife tiri nawo pafupifupi foro handiredi kumeneko, amene akonzeka kuti apemphereredwe.”

<sup>173</sup> Ine ndinati, “Chabwino,” ine ndinati, “mungomupangitsa iye akhale mmbuyo. Chifukwa, ngati iye angapite patsogolo, izo ziyambitsa kuti aliyense wa iwo achite zimenezo.” Ndipo ndinati, “Ife sitingakhoze kuchita zimenezo. Muuzeni iye adzangolowa pamzere mwinamwake mawa. Ife tidzakhala tiri pano mpaka mawa kuti tidzamupatse iye khadi la pemphero.”

<sup>174</sup> Iye anati, “Inu mudzabwere ndipo mudzayesere izo.” Anati, “Ndiri nawo othandizira firii handiredi kumeneko omwe akulephera nkomwe kuti amugwire iye, ndipo,” anati, “sangalemere mapaundi nainte.” Ndipo anati, “Inu simungathe kumugwira iye.” Anati, “Iye akumathamanga pakati pa miyendo yanu, kulumphira pa mapewa awo, kapena chirichonse, ali ndi mwana wakufa uyu.”

175 Ndipo ine ndinati, “M’bale Jack,” ndinati, “Iye sakundidziwa ine. Iye sangandisiyanitse ine ndi inu. Tsikirani kumusiko ndipo mukamupempherere mwanayo, ndipo izo zikhazikitsa izo monga choncho.” Ndipo ine ndinati, “Mwanayo wafa?”

Anati, “Inde.” Ine ndinati. . .

176 Ndinali kuyankhula pa chikhulupiriro kukhala thunthu, thunthu la zinthu zoyembekezedwa. Ndipo ndinali kuyankhula. Ndipo M’bale Espinoza anayamba kuyankhula, pamene ine ndinali kuyankhula. M’bale Jack anayamba kumatsika kuti akamupempherere mwanayo. Ndipo pamene ine ndinayamba kuyang’ana, ine ndinayang’ana kunja kuno patsogolo panga, ndipo apo panali mwana wamng’ono wa ku Mexico, wopanda mano, izo zinali zazing’ono kwambiri. Anali akumwetulira, akundiayang’ana ine, masomphenya.

177 Ine ndinati, “Dikirani miniti, M’bale Jack. Mbweretseni mwanayo kuno.” Ndipo kotero iwo anatsegula njira.

178 Apa anabwera mkazi wamng’onoyo, ali ndi mikanda ya pemphero mmanja mwake, ndipo akugwera pansi, akufuula, “Padre!”

179 Ndipo ine—ine ndinamudzutsa iye. Ine ndinati, “Usatero.” Iye anali ndi kabangete kakang’ono ka buluu ndi koyera, kamizeremizere; mwana wamng’ono, wowuma, wa pafupifupi kutalika *chonchi*, atagona mmikono mwake.

Ine ndinati, “Mufunseni iye kuti wafa liti.”

180 Anati, “Iye anafera mu ofesi ya adokotala, mmawa umenewo, pafupifupi naini koloko.” Ndipo iyi inali pafupifupi hafu-pasiti naini kapena teni koloko usiku umenewo. Ndipo akungonyowa, iye anali atayima; tsitsi lake lonse pansi. Mkazi wamng’ono wokongola, ndipo, iye, mwinamwake mwana wake woyamba. Iye ankawoneka kuti anali usinkhu wa zaka twente-faivi, kapena chinachake.

181 Ndipo ine ndinati, “M’bale Espinoza, musatanthauzire pemphero ili, chifukwa ndangowona kumene masomphenya a ba- . . . kapena mwana wamng’ono kunja uko akundisekerera ine.” Ine ndinati, “Akhoza kukhala mwanayo.”

182 Ndipo ndinadzayika manja anga pa bulangeti laling’onolo, ndipo ndinati, “Wokonedwa Atate Akumwamba, ine sindikudziwa chimene masomphenyawo amatanthauza, koma ndamuwona mwana wamng’onoyo. Ngati mwana ameneyo, Inu mwakonzeka kuti mumuyitanirenso ku moyo, ine ndiyitanitsa moyo wake, mu Dzina la Yesu Khristu.” Analira mokuwa, ndi kugunyuzwa bulangeti limenelo ndipo anayamba kukuwa monga *choncho*. Ndipo ine. . .

183 *Liwu* la Amuna Amalonda linalimba zimenezo, osati kale litali. Ine ndinati, “M’bale Espinoza, musanene kanthu za zimenezo tspano. Inu mumtumize wothamanga

amuthamangire mwana ameneyo ndi mkazi ameneyo, ndipo apite naye kwa adokotala ndipo mukatenge chikalata chosainidwa musasindikize tsopano,” Ndinati, “chifukwa ziyenera kukhala zoon. Ife sitikudziwa.” Chotero, chotero anatumiza wothamanga.

<sup>184</sup> Ndipo adokotala anasaina chikalata chovomerezeka, “Mwanayo anafa ndi chibayo chowirikiza,” mmawa umenewo mu yake...nthawi ya naini koloko muofesi yake. “Iye samapuma. Mtima wake unali utapita, anali atafa komanso atauma.”

<sup>185</sup> Ndipo pamenepo panali mkazi wamng’ono uja. Chifukwa chiyani? Chifukwa anali wakhama. Palibe chimene chikanamuletsa iye. Iye anali wakhama. Iye anali wolimbikira, ngakhale wansembe wake akanamuchotsa iye mu mpingo (ndithudi iye akanatero), ziribe kanthu zomwe zinachitika. Anakhala akuyang’ana ku mpanda, mausiku angapo mmbuyomo, ndipo iye anali atamuwona wakhungu wokalamba uja akulandira kupenya kwake. “Ngati Mulungu anapereka kupenya kwa wakhungu, Iye akhoza kuwukitsa wakufa!” Ndipo iye anali nacho chosowa. Anali wakhama, monga mkazi wa Chisirifonika. Iye anapeza chokhumba chake chifukwa anali wakhama.

<sup>186</sup> M’bale ndi mlongo, ife tiri mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu. Iye anati, “Pomwe pali awiri kapena atatu adzasonkhana mu Dzina Langa, pamenepo Ine ndidzakhhalapo pakati pawo. Chirichonse chimene iwo agwirizanapo, kukhudza chinthu chimodzi, ndi kupempha, iwo adzalandira.” Tiyeni tikhale akhama tsopano mu Kukhalapo kwa Mulungu, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>187</sup> Atate athu Akumwamba achisomo, takhala tikuyankhula kwa pafupifupi maminiti sarte ndi chinachake tsopano, kapena ochulukirapo, chifukwa cha Ufumu Wanu. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Mulungu anapanga lonjezo. Mulungu ndi wokakamizika ku lonjezo Lake. Mutilole ife, Ambuye, tizikumbukira, ndi kukhala monga mkazi wamng’ono uja, khama. Ngati Yesu ali pano pakati pathu, ndiye tiyeni tigwiritsitse kwa Iye mpaka titakwaniritsa zomwe tadzera.

<sup>188</sup> Ngati alipo iwo pano, usikuuno, amene sanapulumsidwe, mulole iwo agwiritsitse mpaka chisomo chopulumutsa cha Mulungu chitawalandira iwo.

<sup>189</sup> Ngati iwo ali pano opanda ubatizo wa Mzimu Woyera, mulole iwo akhale monga mkazi wamng’ono uja, musalole kuti nthawi kapena china chirichonse chiyime m’njira. Iwo adzagwira ndipo adzakhala olimbikira mpaka Mzimu Woyera utazadzitsa moyo wawo ndi chisomo cha Mulungu.

<sup>190</sup> Ngati iwo akudwala, mulole iwo asakalekerere. Mulole iwo akagwiritsitse monga Yakobo, momwe iye analiri wolimbikira.

Iye anagwiritsitsabe, ndipo anati, “Ine sindidzakulolani Inu kuti mupite mpaka Inu mutandidalitsa ine.” Dalitso limenelo linatanthauza moyo kwa iye, ndipo limatanthauzanso kwa ife usikuuno. Ndipo machiritso amatanthauza moyo kwa ife, Ambuye.

<sup>191</sup> Ife tikupemphera kuti Kukhalapo Kwanu kubwere, kuti ife tidzakhoze kukugwirani Inu, ndi Inu kutigwira ife, monga Inu munachitira ndi Yakobo, kalonga wolimbana uja; kuti Inu mutisinthe dzina lathu, kuchokera ku bukhu la mpingo pano pa dziko lapansi, kupita ku Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa Kumwamba. Kulimbikira, kugwiritsitsa mpaka Mulungu atatsimikizira lonjezo Lake mwa ife! Ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

<sup>192</sup> Ambuye, ife tikudziwa kuti Mawu ochokera kwa Inu angatanthauze oposa mamillioni amene wina aliyense angakhoze kuwayankhula. Bwerani, Ambuye, ndipo mudzatsimikizire izi, kuti ine ndanena Choonadi. Inu ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Inu ndinu Mawu. Inu munali Mawu amene anali mwa Nowa. Ndinu Mawu amene anali mwa Mose. Inu munali Mawu amene anali mwa Eliya. Inu munali Mawu amene anali mwa Davide. Inu ndinu Mawu opangidwa thupi ndipo muli pakati pathu usikuuno. Inu muli pano kuti mudzatsimikizire lonjezo lirilonse limene Inu munalipanga pa ora lino. “Monga zinali mmasiku a Sodomu,” malonjezo onse awa amene Inu munawapanga, Inu muli pano kuti mudzawatsimikizire Iwo. Perekani izi, usikuuno, Atate. Ife tiziyang’ana kuti tikuwoneni Inu pano.

<sup>193</sup> Ndiyeno mulole mpingo ufikire mmwamba mwa chikhulupiriro ndi kugwira, ndi kudzati, “Ndine wolimbikira, Ambuye. Ine ndikhala pano ngati woweruza wosalungama yemwe mkazi wamasiyeyo anamugwira.” Ndipo ngati woweruza wosalungamayo, kuti amuchotse mkaziyo, anamupatsa iye chokhumba chake, ndi mochuluka bwanji Atate Akumwamba adzawapatsa iwo amene Iye akuyembekezera kuti awagwire kwa Iye usikuuno? Perekani izi, mu Dzina la Yesu, ife tikupemphera. Amen. Ambuye adalitsike!

<sup>194</sup> Ine ndikufuna kuwona... Billy, kodi unapereka makadi? [Winawake akuyankha—Mkonzi]. Thuu handiredi? Ndi ati amene unapereka lero, H? Tinayambira pati; wani, usiku wathawu, sichoncho ife? [“Inde.”] Tiyeni tiyambire penapake usikuuno. Khadi la pemphero usikuuno ndi H.

<sup>195</sup> Aliyense yemwe ali ndi makadi apemphero, gwiritsitsani kwa iwo. Mwaona, ife tipempherera aliyense. Ingogwiritsitsani, gwiritsitsani ku khadi la pemphero limenelo. Inu munampatsa bambo khadi la pemphero, iye anachiritsidwa sikisite peresenti nthawi yomweyo. Mukuona? Iye amadziwa kuti alowa pa

mzere, kotero iye anangogwiritsitsa ilo. Ndi chifukwa chake ife timawapereka iwo.

<sup>196</sup> Tiyeni tiyambire, tiyeni tiwone, kuyambira...tiyeni tiyambire eyite usikuuno, tiyambire eyite, nainte, handiredi. Ndani ali ndi khadi la pemphero H, H, monga Kumwamba? H, eyite, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tiwone ngati ndiri... Mwinamwake ine ndikulakwitsa. Ife tiyambira kuchokera penapake ndiye. Bwana? Sindinayiwone iyo. [Winawake akuti, "Kumbuyo komwe."—Mkonzi]. Oh, kumbuyo. Chabwino, bwerani kuno, bwana. H, eyite.

<sup>197</sup> H, eyite-wani, ndani ali ndi eyite-wani? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Eyite-wani, cha apa. Kazibwerani, dona.

<sup>198</sup> Eyite-thuu, ndani ali ndi eyite-thuu, kodi mungakweze mmwamba dzanja lanu? Apo pomwe, eyite-thuu? Chabwino, eyite-thuu, ndani ali ndi khadi la pemphero H, eyite-thuu? Pali eyite, eyite-wani; ife tikufuna H, eyite-thuu. Kodi munganene bwanji izo mu Chisipanishi? Akhoza kukhala winawake wachi Spanish. Chabwino, chabwino, eyite-thuu.

<sup>199</sup> Eyite-firii. H, eyite-firii, ndani ali ndi khadi la pemphero H, eyite-firii? Tayang'anani pa khadi lanu la pemphero. Muyang'ane pa khadi la pemphero la woyandikana naye wanu, mwinamwake iwo ndi ogontha ndipo sakumva. H, eyite-firii, eyite-firii?

<sup>200</sup> Osatenga makadi amenewo ngati simuwagwiritsa ntchito. Mukuona? Muziwatenga iwo, ndikuwagwiritsa ntchito. Mukuona? Musakawapereke iwo kwa winawake. Mukawasunge iwo nokha. Inu mudzakanidwa mu mzere wapemphero, mwaona. Chotero mukatenga khadi lanu, muzibwera, muzidzamvetsera malangizo msonkhano usanachitike. Mutenge khadi lanulo ndipo mukatero mukhale pa mpando wanu, mwaona.

<sup>201</sup> H, eyite-firii, ilo liri pati? Eyite-foro? Dona apa. Eyite-faivi, eyite-sikisi. Uko nkulondola, yankhani mwamsanga. Eyite-sikisi, eyite-seveni, eyite-eyiti, eyite-naini. Nainte, nainte-wani, nainte-thuu, nainte-firii, nainte-foro, nainte-faivi, nainte-sikisi, ninte-seveni, nainte-eyiti, nainte-naini, handiredi. Awerengeni iwo, M'bale Grant, ngati mungathe, ndipo muwone ngati iwo onse alowa mu mzere wa pemphero.

<sup>202</sup> Tsopano ine ndimufunsa aliyense muno tsopano. Tikhala titatsiriza mu pafupifupi maminiti teni, fifitini. Ine ndimufunsa aliyense muno kuti akhalebe pampando wanu, yemwe sanaitanidwe. Mukhale molemekeza kwenikweni, mukhale chete. Limbikirani tsopano.

<sup>203</sup> Tiyeni ndikupatseni nkhani ina yaying'ono. Nthawi ina, panali mkazi. Yesu anali...Kutchuka kwake kunafalikira mu Gadara, ndipo mkazi wamng'ono anabwera kumeneko; kapena, osati mu Gadara, linali dziko lina. Ndipo iye anali atamva za Iye. Iye anali ndi vuto la magazi. Iye anabwera ku msonkhano

kumene kunali Yesu, pa gombe la nyanja, koma iye sanakhoze kufika kwa Iye. Ndipo chotero iye ananena mu mtima wake, tsopano mvetserani, mkati mwa mtima wake, kuti, “Ngati ine ndingakhoze kukhudza chovala Chake, ine ndichiritsidwa.” Mukuikumbukira nkhaniyo? Tsopano, iye anazembera nadutsa ndipo anakakhudza chovala Chake.

204 Tsopano chinachitika ndi chiyani? Yesu anatembenuka anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

205 Bwanji, Petro anamudzudzula Iye. Tangoganizani za izo tsopano, pamene iwo akuwona ngati iwo onse alipo. Petro anamudzudzula Iye. Iye anati, “Ambuye!” Chinachake chonga ichi, “Bwanji, anthu azidabwa ngati Inu muli mmalingaliro Anu abwino.”

206 Bwanji, aliyense, “Moni, Rabi! Moni, Mneneri! Uyu ndi Mneneri wachinyamata waku Nazareti? Uyu ndi Mneneri wa ku Galileya? Moni, kumeneko!”

207 “Mutalikirane naye Munthu woteroyo,” anatero ansembe ndi onse a iwo. “Chokaniko kwa Iye, aliyense.”

208 Koma iye anagwiritsitsabe chimodzimodzi basi, iye anatero. Iye anati, “Ngati ine ndingakhoze kokha kukhudza chovala Chake!” Iye anatero.

209 Pamenepo Petro anati, “Chabwino, Inu mukuwapangitsa anthu kuganiza kuti Inu mwasokonezeka.”

210 Iye anati, “Koma Ine ndazikira kuti ndafooka.” Ndi angati akudziwa zimenezo? *Ukoma*, kutanthauza “mphamvu,” zachoka mwa Iye.

211 Ndipo Iye anayang’ana pozungulira pa omvetsera mpaka Iye anamupeza mkaziyo. Ndipo pamene Iye anamupeza dona wamng’ono, kodi Iye ananena chiyani kwa iye? Iye anati, “Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe.” Anamuza iye za vuto lake la magazi, kuti iye anali atapulumutsidwa. Nkulondola uko?

212 Tsopano ndi angati akukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndi angati akudziwa kuti ichi ndi Choonadi? Mu Ahebri 3, amati, “Pakali pano Iye ndi Wansembe Wamkulu amene angakhoze kukhudzidwa ndi zofooka zathu.” Ndi angati akudziwa zimenezo?

213 Chabwino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, . . . Kungoti, Iye sali, mmawonekedwe athupi; pamene Iye adzabwere monga chomwecho, nthawi idzakhala yatha, Iye adzawutenga Mpingo limodzi ndi Iye.

214 Koma Iye ali pano mmawonekedwe a Mzimu Woyera, kuti abwere mwa ine ndi mwa inu, ndi kudzachita ntchito Zake zomwezo. Iye ananena, mu Yohane 14:12, “Iye amene

akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita Iye adzazichitanso.” Ndi kulondola uko?

<sup>215</sup> Ndipo ngati Mawu ali mwa ife, ndipo ife tikunena Choonadi, ndipo ndi Mawu amene Iye anawalonjezera lero, ndiye si Mawu a Mulungu “akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndi Wozindikira zolingirira ndi zamkati mwa mtima”? Kodi Baibulo limanena zimenezo? Kodi aneneri onse samakhoza kuzindikira maganizo mmenemo—mmaganizo a anthu? Nkulondola uko? Chifukwa chiyani? Anali Mawu amene anali mwa iwo, Mawu a Mulungu a tsiku limenelo. Mukuona? Umo ndi momwe iwo ankatsimikizidwira. Izo zinali zowayenereza zawo. Palibe mmodzi wa iwo amene anali wa bungwe, panalibe mmodzi, sanatero nkomwe. Zowayenereza zawo zinali utumiki wawo.

<sup>216</sup> Mulungu anati, “Ngati alipo mmodzi mwa inu, amene ali wauzimu kapena mneneri, ndipo chimene iye anena chikachitika, ndiye mumumvere iye, pakuti ine ndiri ndi iye. Koma ngati izo sizichitika, chabwino, musamumvere iye.” Ndipo izo siziyenera kungokhala kamodzi kokha, ziyenera mosalekeza nthawi zonse; kuchokera kwa aneneri.

<sup>217</sup> Iliipo mphatso ya uneneri, yomwe imakhala mu mpingo, yomwe imayenera kufufuzidwa ndi—ndi ofufuza, izo zisanawuzidwe ku mpingo, ndithudi. “Zizikhala pamaso pa oweruza awiri kapena atatu, ndipo zikatero zikawuzidwe kwa iye.”

<sup>218</sup> Koma mneneri amabadwa ali mneneri, wokonzedweratu, wodzozedweratu. “Yeremiya,” Mulungu anati, “usanawumbidwe ngakhale m’imba mwa amako, Ine ndinakudzozza iwe mneneri pa fukoli.” Yohane M’batizi, zaka seveni handiredi ndi thwelovu iye asanabadwe, “Iye anali liwu lofuula mchipululu, ‘Konzani njira ya Ambuye.’” Mukuona? Ndithudi.

<sup>219</sup> Zindikirani, tsopano, pamene Yesu anali padziko lapansi, Iye anapereka nsembe ya machiritso ndi ya chipulumutso. Kodi ife tikukhulupirira zimenezo? Yesu sangabwere usikuuno ndi kudzakupulumutsani inu; Iye anachita kale zimenezo. Funso la tchimo linathetsedwa. Iye ndi Mwanawankhosa wa Mulungu amene anachotsa machimo a dziko lapansi. “Iye *anavulazidwa* chifukwa cha zolakwa zathu. Ndi mikwingwirima Yake *ife* tinachiritsidwa.” Ndi nthawi yakale. Ziribe kanthu kuti mungafuule mochuluka bwanji, ndipo mungafuule mochuluka bwanji, zimenezo sizingachite ubwino pang’ono pomwe mpaka inu mutavomereza izo.

<sup>220</sup> “Ndipo Iye ndi Wamkulu Wansembe amene wakhala kudzanja lamanja la Ufumu Kumwamba, kuti azichita chitetezero pa chivomerezo chathu.” Muyenera kuzilandira izo ndi kuzivomereza izo. Mwaona, ndiko kulondola. Momwemonso ndi machiritso.

221 Koma bwanji ngati Iye akanakhala kuti akuyima pano usikuuno, atavala suti iyi yomwe Iye anandipatsa ine? Kodi Iye akanachita chiyani mu mzere wa pemphero? Kodi mukanadziwa bwanji kuti anali Yesu? Mukuona? Tsopano, tikanena zakuti wina abwere ndi kudzati, “Yesu, kodi Inu mundichiritsa ine?”

Iye anganene kuti, “Ine ndinachita kale zimenezo.”

222 Tsopano ngati iye anali ndi zipsyera za misomali m’manja mwawo; ndipo aliyense akhoza kukhala nacho icho, mwaona, chipsyera chirichonse chikhoza kukhala.

223 Koma ndi chiyani chimenecho, inu mukudziwa bwanji, kodi inu mukudziwa mtundu wanji wa mpesa umenewo uli? Ndi mtundu wa moyo womwe uli nawo. Ndipo mpesa uliwonse, ngati woyamba . . . Nthambi yoyamba imene inatuluka mu Mpesa umenewo, Yesu Khristu, iwo analemba Bukhu la Machitidwe kuseri kwa iwo. Ndi zoonza zimenezo? Ngati Iyo iti idzatulutse inanso, iwo adzalemba Bukhu lina la Machitidwe. Pakuti ngati inabala mphesa, yoyambayo, nthawi yotsatira iyo siyingakhoze kukhala ndi mandimu. Koma, mpesa wa mandimu ukhoza kukhala mmenemo, ndi chipatso cha citrus. Koma ukukhala mwa iwowokha; iwo nthawizonse uzidzabala mandimu, ndi mpesa womezanitsidwa mwa iwo. Koma ngati Mpesa pawokha ubala nthambi, iwo udzabala chipatso monga woyamba unachitira, pakuti iwo udzakhala Moyo umene uli mwa Yesu Khristu udzakhala mu mpesa umenewo. Ndi choncho.

224 Yesu anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Tsopano ngati Iye akanakhala pano, Iye akanadziwika ndi Moyo Wake, ndi zinthu zimene Iye analonjeza kwa m’badwo uno.

225 Ndi angati anali pano usiku watha, tiyeni tiwone dzanja lanu. Kwenikweni nonse inu, ine ndikuganiza. Chabwino. Tsopano pali anthu . . .

226 Aliyense mu mzere umenewo, monga momwe ine ndikudziwira, ndi mlendo kwa ine. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. Aliyense ndi a . . . Kodi ndinu mlendo? [Munthuyo akuti, “Inde.”—Mkonzi].

227 Ndi angati kunjika uko ali alendo kwa ine? Chabwino. Chinthu chokha chimene ine ndikukupemphani inu kuti muchite ndi kukhala ndi chikhulupiriro ndi kukhulupirira kuti ine ndakuwuzani inu Choonadi.

228 Tsopano, taonani, Khristu analonjeza zinthu izi kwa masiku otsiriza. Tsopano, ndikudziwa kuti mwakhalapo ndi ankhondo akulu mu mzinda muno, mwinamwake Oral Roberts ndi, oh, monga malemu Jack Coe ndi amuna aakulu aja achikhulupiriro; iwo anakhala moyo nthawi yawo. Koma kumbukirani chizindikiro chotsiriza chimene dziko la Amitundu linachiwona mwana wolonjezedwayo asanabwere mu nthawi ya Abrahamu, yemwe ali atate wa onse, ndipo Yesu analonjeza chinthu

chomwecho; chizindikiro chotsiriza chimene chinasonyezedwa kwa Mpingo wosankhidwa, tsopano kumbukirani, panali Mmodzi. Awiri anapita uko nakalalikira mu Sodomu, iwo sanasonyeze konse chizindikiro ichi; ngakhalenso lero. Koma kwa Mpingo wotulutsidwa, chizindikiro chinawonetsedwa; ndipo chomwechonso Yesu ananenera kuti chidzakhala chinthu chomwecho, mwaona, Mulungu akuwonetseredwa mu thupi, mwaona, kuzindikira maganizo amene ali mu mtima. Mwaona? Tsopano, Iye analonjeza zimenezo! “Zonse miyamba ndi dziko lapansi zidzalephera, koma Iwo sadzatero.”

<sup>229</sup> Tsopano ngati Iye ati adzawonetsere zimenezo, kusonyeza kuti Iye ali pompano, ndi angati a inu muti mumukhulupirire Iye chifukwa cha machiritso anu ndi chirichonse chimene inu mukuchisowa?

<sup>230</sup> Tsopano, Ambuye Yesu, tsopano ziri kwa Inu, Atate. Chirichonse chimene chiri chifuniro Chanu, chiloleni icho chichitidwe. Ine ndine wantchito Wanu. Awa onse ndi antchito Anu, kapena ambiri a iwo mkati muno. Aloleni iwo amene sali antchito Anu, mwa Kukhalapo Kwanu... podziwa kuti mwinamwake usanafike mmawa iwo adzayenera kuyang’ana pa nkhoze Yanu. Tsopano Inu mukhoza kumwetulira pa iwo ndi chisomo, koma ndiye Inu mudzakhala woweruza wawo.

<sup>231</sup> Mulole zichitike, Ambuye, kuti Yesu abwere pakati pathu, usikuuno, ndi kudzachita ndi kuchita monga Iye anachitira pamaso pa kupachikidwa Kwake; chidzakhala chitsimikizo kwa ife, pamaso pa zipembedzo zonse zachikunja, kuti Mpulumutsi wathu sanafe, koma wauka kwa akufa. Ndipo zitatha zaka zikwi ziwiri, Iye ali basi wamoyo usikuuno monga Iye anali nthawi imeneyo. Ndipo mulole ife, monga iwo aku Emau, tinene kuti, “Kodi mitima yathu siinantenthe mkati mwathu, pamene Iye amayankhula nafe panjira?” Mulole Kukhalapo Kwanu kuzindikirike. Mulole ife tikuwoneni Inu, usikuuno, mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chanu. Ndiyeno mulole anthu akhulupirire ndiye, Ambuye, chifukwa cha Kukhalapo Kwanu kwakukulu kolemekezeka. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

<sup>232</sup> Tsopano ndikutenga mzimu uliwonse... Aliyense wa inu ndinu mzimu. Kumbukirani, simunandiwonepo ine; inu mukuona chotopa chakale ichi apa chimene chikunena Liwu ili. Tsopano Liwu ili mwina likuchokera kwa Mulungu, kapena siliri, mofanana ndi lanu. Liwu ili langodzaza mu chikopa ichi, chomwe ndidzachisinthana ndi china chatsopano chomwe sichidzakalamba. Koma, mzanga, mmodzi aliyense, mzimu. Koter pamene inu musuntha, mwawona, pamene mukhala ndi ulumuliro pamenepo, mwaona, izo zimasokoneza. Ingokhalani bata kwenikweni, mukhale mu pemphero. ndikufuna inu... Ngati Mulungu achite chinachake, tiyenera tikhale othokoza kwa Iye. Ndithudi. Mtamandeni Iye, mukatero mukhale

olemekeza ndi kumayang'anira. Mungokhala bata kwenikweni, ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse.

<sup>233</sup> Tsopano inu kunjira uko amene mulibe makadi apemphero, ziribe kanthu komwe inu muli, inu mungokhulupirira ndi kunena izi, “Ambuye Yesu, zomwe anatiuza ife, ziri mu Baibulo. Ife. . . Ine ndikudziwa kuti Inu munalonjeza izo, ndipo ine ndikudziwa izo ziyenera kukhala Inu. Zimenezo sangakhale munthu ameneyo; iye ndi munthu monga ine ndiriri, kapena monga mwamuna wanga, kapena monga mwana wanga, kapena m'bale, kapena zina zotero.” Mukuona?

<sup>234</sup> Koma mphatso si chinachake, mpeni, umene mmawutenga ndi kupita nawo kukachita zinthu, mphatso. Ena a masiku awa, ndidzatenga hema wamkulu ndikubwera ku mzinda, ndi kudzangokhala kwa pafupifupi miyezi pa nthawi, mwaona, ndi kudzaphunzitsa, chonchobe. Mphatso, ndiyo kudzichotsapo wekha panjira, kotero kuti Mulungu akhoze kubwera mkatimo, kuwona zomwe Iye akuwonetsa, zomwe Iye akuchita. Mphatso si, “Ndiri ndi mphamvu kuti ndichite *izi*, ndiri ndi mphamvu!” Mphamvu yanu ya mphatso ndi kuzichotsapo nokha panjira. Ndipo mphatso yomwe Mulungu wakupatsani inu, imagwira ntchito kudzera pamenepo ndiye, mwaona, inu mutachokapo panjira. Mukuona?

<sup>235</sup> Tsopano, ine sindingakhoze kumupanga Iye kuti andiuze ine kanthu. Iye ayenera kuti achite zimenezo. Tsopano kuti tisunge nthawi. . . Ndachedwa kwenikweni.

<sup>236</sup> Koma bwerani kuno, dona, ine ndikufuna kuti inu muyime pomwe pano. Ine ndinali kuyankhula mphindi zingapo zapitazo za mkazi ku. . . pa chitsime. Kodi munali kuno usiku watha? [Mlongo akuti, “Ayi, bwana.”—Mkonzi]. Inu simunali pano. Kodi munayamba mwakhalapo mu umodzi wa misonkhano m'mbuyomu? [“Ayi, bwana.”] Simunakhalepo nkale lomwe. Iyi ndi nthawi yake yoyamba. Ndife alendo. Iye panalibepo nkomwe pano usiku watha. Panalibepo malangizo pa zimenezo. Palibepo koma kungoti imirirani apa. [“Ndi choncho.”] Tsopano ife taima. Mukukumbukira nkhani ya mkazi pachitsime? [“Inde, bwana.”] Pamawoneka chinachake pang'ono monga chonchi, ndipo Mwamuna ndi mkazi anakumana kwa nthawi yawo yoyamba m'moyo.

<sup>237</sup> Tsopano, mkazi uyu anali mkati, iye anali mkati. . . Iye anali mu manyazi. Iye anali atakwatiwa nthawi zambiri, ndipo iye—ndipo anali kukhala ndi mwamuna yemwe sanakwatiwe naye, ndipo—ndipo chinali chinthu choipa kwambiri. Ndipo Yesu anayankhula naye iye.

<sup>238</sup> Tsopano inu mukukumbukira, Iye anati, mu Yohane Woyera 5:19, “Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangakhoze kuchita kanthu mwa Iyeyekha; koma chimene awona Atate akuchichita, chomwechonso Mwana adzachita.” Chotero, Yesu

sanachite chinthu chimodzi popanda choyamba kuchiwona icho mu masomphenya, kapena Iye ananena chinachake cholakwika pamenepo. “Mwana samachita kanthu mpaka Iye atawawona Atate akuchita izo poyamba.” Osati *kumumvera* Iye; “amamuwona Iye akuchita izo.” Ndiyeno Atate. . .

<sup>239</sup> Iye anasowa kuti apite ku Samariya. Iye anali akupita ku Yeriko, koma Iye anapita ku Samariya, mzinda wa Sukari. Ndipo Iye anakakomana ndi mkazi uyu, ndipo Iye anayamba kuyankhula ndi iye mpaka Iye anapeza pamene vuto lake linali. Ndiye Iye anamuza iye vuto lake, ndipo mwamsanga, iye mu chikhalidwe chimenecho, iye anazindikira kuti icho chinali chizindikiro cha Mesiya.

<sup>240</sup> Chabwino, ngati uyo ali Iye dzulo, akanakhala Mmodzi yemweyo lero, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndi zoon zimenezo, omvetsera? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Mukuona?

<sup>241</sup> Tsopano tikukumana kwa nthawi yathu yoyamba. Ine sindine Iye, ndipo inu sindinu mkaziyo, koma Iye akadali Mulungu. Ndiko kulondola, mwaona. Tsopano ngati inu mungakhoze kukhala ndi chikhulupiriro mu—mu zimene ine ndikunena, mu Mawu! Ine sindidzanena konse kanthu koma zomwe ziri mu Mawu awa. Iye akhoza kuchita zinthu kunja kwa Mawu amenewo; koma utali wonse pamene Iye achita Izo, ine ndikudziwa Ndiko kulondola, ndiye, mwaona. Ndipo tsopano inu simukundidziwa ine, ine sindikukudziwani inu.

<sup>242</sup> Ndiye chotero ngati mukudwala, ndipo ine ndinaika manja pa inu, ndipo ndinafuula, monga wankhondo wamkulu uja, M’bale Roberts, kapena ena a iwo, M’bale Allen kapena ena a amuna amenewo, kuyika manja pa inu ndikuti, “Aleluya, Ambuye akuchizani inu,” zimenezo ndi zabwino. Inu mukakhulupirira zimenezo, ndipo izo zigwira ntchito. Mukuona? Mukuona? Koma tsopano bwanji ngati Iye atayima apa ndi kunena chinachake chimene inu mwachita, kapena chifukwa china chimene inu mukudwala, kapena chinachake chomwe chachitika kudutsa mmoyo, kapena chinachake chimene simumayenera kuchichita? Oh, kuti izo, inu mukanadziwa kuti izo zimayenera kukhala zolondola, zomveka bwino kwa malingaliro anu ndiye. [Mlongo akuti, “Ndi choncho.”—Mkonzi]. Uko nkulondola.

Zingakhale zanu, kunja uko?

<sup>243</sup> Tsopano kodi ndikuyankhula naye chiyani mkaziyo? Mwaona, ine sindinapitirize pa uthenga umenewo usikuuno (ine ndiyenera kulimbikira), mwaona, izo zingandisinthe ine kuyamba kulalikirira. Ndipo tsopano ndiyenera ndibwerere ku kuzindikira zamumtima, kudzitsitsimutsa ndekha, kumutengera William Branham kumbali.

<sup>244</sup> Ndi angati anayamba anawonapo chithunzi icho chimene chinajambulidwa kuno ku Houston? Ndi inunso... Chiri pano. Icho chiri patsogolo apa tsopano, mwaona. Chimene chapachikika pambali pomwe, pakati pa ine ndi mkaziyo, pakali pano. Ndi Icho pamenepo, chikungozungulira zungulira. Ngati mkaziyo akufuna kuti achitire umboni kwa zimenezo; iye akudziwa, mu mphindi pang'ono zotsiriza zapitazi, pakhala pali chinachake chonga kumverera kokoma kwenikweni. [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu. ["Ameni. Amene."] Mukuona? Ine ndikuyang'ana kumene pa Icho. Mwaona, ziri ngati kukhala mu gawo lina. Ine ndikuchiyang'ana Icho, kudzera mwa mkaziyo.

<sup>245</sup> Tsopano, donayo, chinthu chimodzi, iye ali ndi manjenje kwambiri. Ndipo ndi chimene mumafuna kuti ndipempherere. Ndipo chimenecho ndi choyambitsidwa mwachibadwa basi chifukwa cha nthawi iyi ya moyo yomwe mukukhalamo, kulowa mu m'badwo uno ndi zina zotero, zimenezo zikukupangitsani inu wamanjenje.

<sup>246</sup> Chinthu chinanso, inu muli ndi chinachake kumbali yanu, izi—ziri ngati matumba aang'ono a mpweya, monga, umasonkhana m'mbali mwanu. Tsopano nkulondola uko? [Mlongo akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Kwezani mmwamba dzanja lanu, ngati izo... ["Ndizo—ndizo zonenena zochokera kwa adokotala."] Mukuona?

<sup>247</sup> Tsopano, onani, tsopano pamenepo ndi zimenezo kachiwiri, winawake akuti, "Iye anapeka." Inu, ine ndidzatchula yemwe uyo ali, limodzi la masiku awa, mwaona. Musachite zimenezo. Inu simungakhoze kudzibisa nokha tsopano, kumbukirani, mwaona. A—Mawu, Iwo ali pano, Iwoeni. Osati ine, mzanga; ndine m'bale wanu basi. Koma Mawu ali pano.

<sup>248</sup> Apa, iye ndi munthu wabwino, tiyeni tiwone ngati ine ndikuganiza zimenezo. Ine sindikudziwa tsopano zomwe ndinanena. Izo ziyenera zidzabwere kudzera pa tepi imeneyo, pakuti ine ndikudziwa zimenezo. Tsopano mphindi yokha. Inde. Inde, iye—amachita manjenje, chomwe ndi chimene chikuyambitsa a—nthawi, usinkhu wake ndi zinthu. Iye ali...

<sup>249</sup> Ndiyeno, chinthu china, inu mwakhala muli ndi—opareshoni. [Mlongo akuti, "Inde, bwana, ndinatero."—Mkonzi]. Ndipo icho chinali chochitika chachikazi, nthawi ina kalelo. Ndi choncho. Zimenezo zinakupangani inu wamanjenje kuposa kale. Ndiko kulondola, sichoncho? ["Inde, bwana, ndi choncho."] Uh—huh, ndiko kulondola. Ndipo izo zinakupangani inu wamanjenje, chifukwa, pa nthawi iyi ya moyo, zinakupangani inu wamanjenje kwambiri. Tsopano, inu mukuganiza kuti ine ndikupeka zimenezo? ["Ayi."]

<sup>250</sup> Pano pali chinthu china. Pali a—mtsikana ndi inu, mtsikana wamng'ono. Ndipo iye ali pano, ndipo akuvutika ndi makutu

otupa. [Mlongo akuti, “Inde. Ameni.”—Mkonzi]. Nkulondola uko? Wakhala kunja uko. Ndipo apo pali mkazi, mkazi wina, bwenzi wa inu, ndipo ali ndi kupsyinjika kwa ubongo [“Inde.”], monga manjenje ndipo kenako misala. Ndi kulondola uko? [“Aleluya!”] Tsopano pamene mutabwerere, mukaike mpango umenewo pa iwo; makutu otupawo akachokapo ndipo akathana nazo izo, ndipo mukakhala bwino. Pitani, mukukhulupirira mu Dzina la Ambuye Yesu.

<sup>251</sup> Kodi mukukhulupirira? Ameneyo anali Yesu dzulo, ndi Yesu lero! Inu muyenera kudziwa kuti ameneyo ndi Winawake, mwaona. Eya. Winawake watero. Tsopano, pamenepo, penyani, uko kunali kumbuyo kwanga. Mukuona? Mukuona? Si... Sindinatha kuchita zimenezo. Inu—inu mukudziwa kuti iyenera kukhala Mphamvu ina, sichoncho inu? Kodi inu mukukhulupirira kuti ndi Ambuye Yesu, molingana ndi lonjezo Lake? Ambuye akudalitseni inu.

<sup>252</sup> Muli bwanji, dona? Ndine mlendo kwa inu, aponso. Ine sindikukudziwani. Ine sindinayambe ndakuwonanipo inu mmoyo wanga. Ndife alendo. Iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukumana, monga momwe ine ndikudziwira. Koma tsopano ngati Ambuye Yesu angandiuze ine chinachake chokhudza inueni, kuti chinachake chonga dona uyo apo, chirichonse chimene chinali, kodi inu mungakhulupirire kuti anali Ambuye Yesu mmalo mwa... Sizingakhale ine, inu mukudziwa. Ndipo tsopano inu mukhoza, monga Afarisi, kunena kuti, “Ndi Belezebule, mzimu woipa.”

<sup>253</sup> Ndipo chifukwa chakuti iwo ananena kuti Mzimu wa Mulungu, umene unali kuchita ntchito imeneyo mwa Iye, unali “mzimu woyipa,” chinali kuchitira mwano motsutsa Mzimu Woyera, chimene sichidzakhulukidwa konse pamene Iwo udzabwere mu tsiku lino. Ndi chifukwa chake fuko lino layima mu chiweruzo lero. Palibe china chatsalira kwa ilo koma chiweruzo. Ilo ladzaza ndi Jack Rubys, ndi ena otero, kotero izo sizingakhoze kukhala chirichonse chimene chingachitike kwa ilo koma chiweruzo.

<sup>254</sup> Tsopano inu mukudwala. Mwakhala mukupita kwaa dokotala. Iye ndithudi angalangize opareshoni. Opareshoni imeneyo ndi ya thumbo. Izo nzoona, sichoncho izo? [Mlongo akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

<sup>255</sup> Pano pali chinthu china. Inu muli mosimidwa kufunafuna chazimu... Inu mwakhala musakupeza bwino. Mwakhala ngati mwabalalika, pang’ono, ndipo mukufuna mubwererenso. Chabwino, inu mwabwerera tsopano. Tsopano pitani, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndipo mukakhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Machimo ako akhululukidwa kwa inu. Tsopano pitani, mukukhulupirira.

<sup>256</sup> Tsopano, sindinanene kuti, “machimo akhululukidwa.” Iye ananena izo. Mwaona, sindinali ineyo. Uyo anali Iyeyo, mwaona.

<sup>257</sup> Kodi inu mukukhulupirira? Tsopano izo ziyenera kukupangitsani inu nonse kudziwa kuti ndi Iyeyo pano. Si zoonza zimenezo? Ngati inu mutangokhulupirira! Mungokhala ndi chikhulupiriro. Osakayikira. Mukhale olemekeza ndi kumukhulupirira Mulungu. Tsopano, onani, inu muli mu Kukhalapo Kwake.

<sup>258</sup> Tsopano, ngati chimodzi cha kuzindikira zamumtima icho chinamupangitsa Mwana wa Mulungu kunena kuti, “ukoma watuluka,” kodi inu mukuganiza kuti izo zingachite chiyani kwa ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo Chake? Mukuona? Izo zingatero, inu mukudziwa chimene izo zingakhale.

<sup>259</sup> Mphindi chabe, si mkaziyo. Ndikuti, inu amene mwachiritsidwa kumene, pamenepo, dona, mukubwerera ku mpando wanu, tayang’anani kwa ine mphindi yokha. Pamenepo pali a—mwamuna wakhala patsogolo panu pomwe apo, yemwe ali ndi vuto la nkusani, wakhala apo pomwe. Eya. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Mukutero? Chabwino.

<sup>260</sup> Ndiuzeni zomwe anakhudza. Ine sindikumudziwa mwamunayo, sindinamuwonapo iye mmoyo wanga. Ngati izo ziri zoonza, gwedezani dzanja lanu, ngati ndife alendo kwa wina ndi mzake.

<sup>261</sup> Tsopano, penyani, kuti inu mukhoze kudziwa chinachake. Mkazi wake wakhala pafupi ndi iye pamenepo, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiiza ine chimene chavuta ndi iye? Kodi inu mundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena wantchito Wake? Kodi inu muchita zimenezo?

<sup>262</sup> Ali ndi chimfine. Ngati ndiko kulondola, kwezani mmwamba dzanja lanu, dona. Chabwino. Tsopano ngati awiri nonse mungakhulupirire! Inu munakhudza Chinachake. Khulupirirani tsopano, ndipo izo zikusiyani inu.

<sup>263</sup> Kodi inu mukukhulupirira Mulungu? Musakayikire. Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

<sup>264</sup> Pano pali mwamuna. Ine sindinayambe ndamuwonapo munthu uyu. Iye ndi wamng’ono kwambiri kuposa ine, ndipo sindinayambe ndamuwonapo kale. Ngati ndife alendo, bwana, kwa wina ndi mzake, kwezani mmwamba manja anu. Chabwino. Sindinayambe ndamuwonapo.

<sup>265</sup> Tsopano titenge chithunzi, mu Baibulo, tiyeni titenge liti...pamene Yesu anakumana ndi Simoni Petro. Ine ndikanamulingalira iye kukhala mwamuna chinachake cha usinkhu umenewo, tsitsi lake likuwonda, pamene Yesu

anakomana naye iye. Tsopano penyani. Iye anayankhula naye iye.

<sup>266</sup> Tsopano, ngati ine sindikumudziwa munthuyo, sindinayambe ndamuwonapo iye, awiri tonse ndi manja athu mmwamba, ndife alendo kwathunthu kwa wina ndi mzake. Tsopano, enawo anali akazi, tiyeni tiwone za mwamuna uyu.

<sup>267</sup> Tsopano inu mundiyang'ane ine, mphindi yokha, ngati m'bale wanu. Ndipo tsopano ngati Ambuye anganene chinachake chimene inu mwachita, kapena chinachake chimene inu mukanayenera kuchita, kapena sakanayenera kuti achite, kapena chirichonse chimene icho chiri, inu mudzadziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi. Inu mukanadziwa. Ndiyeno ngati Iye angakhoze kukuuzani inu chimene chiri cholakwika ndi inu, kapena chinachake chimene chiri mmalingaliro anu, chimene kudwala kwanu kuli, kapena—kapena chinachake chonga icho, kukuuzani inu chinachake chimene inu—inu mudzadziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi. Ndiye ngati Iye angakhoze kukuuzani inu zomwe zakhala ziripo, ndipo inu nkudziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi; ngati Iye akuuzeni inu chimene chiti chidzakhale, ndiye inu mudziwa kuti izo ziyenera kukhala zoonza.

<sup>268</sup> Tsopano izo zingampange aliyense pano. . . Ndikungotenga nthawi yanga ndi bambo uyu, ndi kuyankhula naye iye. Ichi ndi choyamba.

<sup>269</sup> Tsopano inu muyang'ane mbali iyi, mphindi yokha, pamene ife tikuyankhulana. Ambuye andithandize ine tsopano. Ndipo kodi mumakhulupirira kuti zimene Baibulo limanena ndi zoonza? [M'baleyo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi].

<sup>270</sup> Inu mukukhulupirira kuti ino ndi ora limene Yesu alinkudza; kuti Mpingo wachokera ku kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, basi monga piramidi monga kubwera kumeneko? Ndipo tsopano mwala wapamwamba uyenera kukhala wangwiro kwambiri mpaka, pamene Mwalawapamutu uzibwera, iwo udzayenera kudzagwirizana ndi izo. Utumiki uyenera kuyamba *chomwechi* ndi kumangobwera kwa ochepa nthawi zonse, kumapeza magulu aang'ono, ndi gulu laling'ono, mpaka potsiriza Mwala kukumana ndi nyumbayo. Iye ali Mwalawapamutu, akutenga nyumba yonseyo limodzi ndi Iye, imene ili Mpingo. Onse a iwo adzawuka, mmbuyo momwe kuchokera pa ulonda woyamba uwu, mpaka ku wachisanu ndi chiwiri, ndipo onse adzapita mu Mkwatulo. Aliyense anali ndi tsiku lake loyikidwa kwa iwo, ndipo iwo anali nawo okonzanso awo ndi oyambitsa, ndi zina zotero, kudutsa monse. Ndipo tsiku lotsiriza ili, izo zabweranso mwa mphungu kachiwiri, zomwe ziri kubwerera mu m'badwo wauneneri, kukazibweretsa izi pamodzi.

271 Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, Mawu ndi Mwala, Mmodzi wakudzayo? [M'baleyo akuti, "ndikutero."—Mkonzi]. Inu muli ndi kumverera kwabwino kwambiri kwa inu, bwana.

272 Tsopano, vuto lanu ndi chiyani, munachita ngozi. Pa ngozi imeneyo, munatenthedwa ndi mpweya wa carbon monoxide. Zimenezo nzoona. Zinakupatsani poizoni. Zinakupatsani poizoni mchiwindi chanu, ndipo munali nacho vuto. Munali ndi vuto ndi mmimba mwanu. Inu munali ndi vuto ndi mtima wanu. ["Kulondola."] Ndipo zakupangitsani inu kukhala wamanjenje kwambiri mpaka munadziyambitsira nokha kuyipidwa. Ndinu wosauka, muyenera mubwerere ku ntchito. Koma mukuwopa kubwerera ku ntchito, mukuwopa mpweya wa carbon monoxide umenewo. Koma zikakhala bwino. Tsopano, kumbukirani, ngati—ngati Yesu Khristu andiwuze ine yemwe inu muli, adzatero... Tsopano zinthu zimenezo zinali zoono, sichoncho izo? Ngati Iye ati andiwuze ine yemwe inu muli, kodi inu muvomereza zimenezo ndi kumadziwa, ndi kumabwerera kwanu ndi kukakhala wosangalala? Kodi muchita zimenezo? Dzina lanu ndinu Bambo Wagner. Bwererani kwanu, panjira yanu.

273 Kodi mukukhulupirira tsopano? Ndi mtima wanu wonse, inu mukukhulupirira? "Ngati inu mungakhoze kukhulupirira, zinthu zonse ziri... Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira."

274 Tsopano kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizirani vuto lachikazi limenelo? Tsopano ingopitirirani pa nsanja mukuti...?... Amen. Mukuona? Mulungu akudalitseni inu.

275 Tsopano, dona, pamene inu mudzuka mmawa, inu mumakhala wowuma, inu mumalephera nkomwe kuti musunthe pozungulira mochulukira, nyamakazi. Koma kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza nyamakazi? [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino, pitani panjira yanu, mukuti, "Zikomo Inu, Ambuye." ["Koma ine—sindinatero... Ndimasowa machiritso a mitsempha."] Chabwino, bwana, ndi chimene chimayambitsa nyamakazi yanuyo, mwaona, inali misempha yanuyo. "Ngati mungathe kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheka," koma choyamba inu muyenera kukhulupirira zimenezo.

276 Kodi mukuganiza chiyani, bwana? Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza vuto la mtima ndi kukupangani inu kukhala bwino? [M'baleyo akuti, "Ndithudi ndikutero!"—Mkonzi]. Chabwino, pitani panjira yanu, muziti, "Zikomo Inu, Ambuye Yesu."

277 Tsopano, dona, inu mwaphimbidwa, zimenezo zikutanthauza khansa. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu

achiza khansa? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Chabwino, vomerezani izo ndipo mupite panjira yanu, mukuti, “Zikomo Inu, Wokondedwa Mulungu,” ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

<sup>278</sup> Mulungu akhoza kuchiza vuto la mmimba, kapena china chirichonse. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Mlongo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi]. Chabwino, pita panjira yanu, ndipo zisangalalani, mukuti, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu.”

<sup>279</sup> Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza vuto lanu lachikazi, kuwukha kumeneko? Chabwino, kazipitirirani panjira yanu, mukuti, “Ambuye Alemekezeke.” Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

<sup>280</sup> Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza nkusani ndi mphumu, ndi zinthu zonse izi, kukupangani inu kukhala bwino? Pitani panjira yanu, mukukondwera, mukuti, “Zikomo Inu, wokondedwa Mulungu.”

<sup>281</sup> Bwanji ngati ine ndikanati ndisanene kanthu kwa inu, kungoika manja pa inu, inu mukanakhulupirira izo? Mu Dzina la Ambuye Yesu, muchiritsidwe. Khulupirirani ndi mtima wanu wonse.

<sup>282</sup> Bwerani, dona. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Chikhalidwe cha kuchepa magazi ndi vuto la mtima, kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Ngati mukutero, pitirirani panjira yanu, muziti, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu,” ndipo mukakhale bwino.

<sup>283</sup> Chabwino, bwana. Bwerani, dona. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiritsa matenda a shuga ndi kuwapanga anthu kukhala bwino ku matenda a shuga? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Ndiye zipitani panjira yanu, mukuti, “Zikomo Inu.” Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, mwaona.

<sup>284</sup> Mulungu amachiza manjenje ndi vuto la mmimba, aponso. Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye akuchizani inu? Pitani panjira yanu, mukukondwera. Mukadye chakudya chamadzulo chanu, ndipo mukakhale wa kulimbika kwabwino.

<sup>285</sup> Bwerani. Mmimba mwamanjenje, aponso. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? [Mlongo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi]. Pitani panjira yanu, ndipo mukadye, ndiponse muchiritsidwe. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

<sup>286</sup> Muli ndi kugunda kwa mtima pang’ono, komanso mumakhala ngati muli ndi nyamakazi. Inu mukumukhulupirira Mulungu, Mulungu akuchizani inu? [Mlongo akuti, “Inde, ine ndikutero.”—Mkonzi]. Pitani panjira yanu, ndipo mukukondwera, ndikumati, “Zikomo Inu, Ambuye.”

287 Mmimba mwamanjenje mmene mukuyambitsa zilonda za m'mimba ndi zinthu. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu kukhala bwino ndi kukuchizani inu? [Mlongo akuti, "ine ndikutero."—Mkonzi]. Pitani panjira yanu, ndipo muziti, "Zikomo Inu, Ambuye," ndipo mukakhale bwino.

288 Muli ndi zinthu zambiri, vuto la udona. Chimodzi mwa zinthu zanu zazikulu ndi vuto la mtima, muchuluka kwambiri pozungulira mtima wanu. Kodi mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Pitani panjira yanu, ndipo mukusangalala, ndi kumati, "Zikomo Inu, Ambuye."

289 Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza nyamakazi? [Mlongo akuti, "Inde, bwana."—Mkonzi]. Kazipitirirani kumapita, ndipo nyamakazi yanu ichokapo.

290 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Mukuona? Ndithudi zimenezo. . .

291 Tsopano ena a inu kunja mwa omvetsera. Tsopano khalani molemekeza. Khalani olemekeza, ingokhalani chete, inu mukhulupirire ndi mtima wanu wonse tsopano. Yang'anani mbali iyi, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ena a inu anthu kunja uko omwe simukhala mu mzere wa pemphero.

292 Mnyamata wamng'ono uyu wakhala pansu apa, munthu wamng'ono wonenepa wakhala apo pomwe. Kodi inu simukuwona Kuwala kumeneko pa iye? Munthu wamng'onoyo akuvutika ndi vuto la impsyo. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiza vuto la impsyo, mwanawe? Iwe ukukhulupirira zimenezo? Chabwino, imirira pa mapazi ako ndipo unene kuti, "Ine ndikuzikhulupirira izo ndipo ndikuzilandira izo." Chabwino. Mulungu akudalitse iwe. Kazipita kwanu. . .

293 Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? "Ngati mungathe kukhulupirira, zinthu zonse ndi zotheke."

294 Nanga bwanji inu amene munangokhala pansu apo, munabwera ndi mnyamata wamng'onoyo ndipo munadzakhala pansu? Kodi inu mukukhulupirira, vuto la diso limenelo, Mulungu achiza vuto la diso lanu ndipo akupangani inu kukhala bwino? Inu mukutero? Chabwino, inu mukhoza kukhala nawo machiritso anu, inunso. Chabwino. Munangokhala pansu pa nthawi yoyenera. Amen. Kazipitirirani patsogolo. Ziri bwino. Izo nzabwino. Chabwino. Amen. Chabwino.


295 Dona yemwe ali pafupi ndi inu pamenepo, iye ali ndi vuto ndi mutu wake. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza vuto la mutu wanu, dona? [Mlongo akuti, "ine ndikutero."—Mkonzi]. Chabwino. Mtsikana wanu wamng'ono apo akuvutika ndi vuto la ubongo. Uko nkulondola, sichoncho izo? Ikani dzanja lanu pa iye, ndipo mukhulupirire, ndipo iye akhala bwino, nayenso. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

<sup>296</sup> Dona wotsatira uyu wakhala motsatira, iye akupemphera, pafupi pomwe ndi iye. Iye akupemphera kumeneko chifukwa cha banja losweka. Ndi zoonza zimenezo, dona? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mukhulupirire, ndipo nyumba yanu idzabwezeretsedwanso. Khalani ndi chikhulupiro.

<sup>297</sup> Dona wakhala pafupi ndi iye ali ndi chotupa. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza chotupa chimenecho, dona? Kwezani mmwamba dzanja lanu, mulandire zimenezo.

<sup>298</sup> Dona wakhala pafupi ndi iye ali ndi vuto la kummero. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza kummero kwanuko, dona? Kwezani mmwamba dzanja lanu.

<sup>299</sup> Chavuta ndi chiyani ndi anthu inu? Kodi inu simukuwona kuti Yesu Khristu . . . Tiyeni tiyimirire pamapazi athu. Imirirani pamapazi anu ndipo mumulandire Yesu ngati mchiritsi wanu.

<sup>300</sup> O Mwanawankhosa wa Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, mchiritseni munthu aliyense pano, kwa ulemelero Wanu. 

64-0305 Kulimbikira  
Soul's Harbor Temple  
Dallas, Texas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)